

CHIOMBOLO MWA MAGAZI



Zikomo inu, mwachifundo. Usiku wabwino, abwenzi. Ndi chamwayi kuti tiri pano usikuuno, kuti ndidzakuyankhuleni inu kachiwiri mu Dzina la Ambuye wathu Yesu Khristu wokonedwa. Ndipo nthawizonse ndi chamwayi kukomana ndi anthu a Mulungu, kulikonse, ndi kuyankhula za Dzina lalikulu ilo, Yesu.

² Ine ndithudi ndikuyamikira nyimbo yomwe m'bale wathu wangoyiimba. Iyo, iyo ndi yoyikonda yanga. Mu tsiku limene iwo akuyesera kuti amupange Yesu kungokhala mneneri wamba chabe, kapena munthu wabwino, kapena mphunzitsi, izo zikuutulutsa kwenikweni Umulungu Wake, chomwe Iye anali. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti Iye ali . . .

³ Sipanayambe pakhala konse Mmodzi wonga Iye, pa dziko lapansi, sipadzakhala pali konse. Iye anali Emmanuele. Iye anali Alfa, Omega; chiyambi ndi mapeto; Iye yemwe anali, yemwe ali, ndipo adzadza; Muzu ndi Mphukira ya Davide; Nyenyezi ya Mmawa. Mwa Iye munali Umulungu. Mwa Iye munali Mulungu.

⁴ “Mulungu anali mwa Mwana Wake, mwa Khristu, akuliyanjaniitsa dziko kwa Iyemwini.” Yesu anati, “Si Ine amene ndikuchita ntchitozi, koma ndi Atate Anga omwe akukhala mwa Ine. Atate Anga ndi Ine ndife mmodzi,” Mulungu anawonetseredwa, mu thupi. Ndi vumbulutso lodabwitsa bwanji la chikondi cha Mulungu kwa ife, Iye kudzifutukula Yekha ndi kubwera pansu ndi kudzakhala mu mnofu wa umunthu, polinga kuti achotse tchimo ndi matenda kwa mtundu wa anthu, ndi kutiombola ife kubwerera kwa Atate. Izo ndi zodabwitsa, si choncho? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ife ndithudi tikuyamikira izo.

⁵ Tsopano, usiku watha, ine ndikulingalira ine ndiyenera kuti ndikhale ngati ndapepesa. Ine . . . Billy anandipeza ine, mofulumira pang'ono, usiku watha, chifukwa zinali ngati . . . Ine ndinafooka. Koma misonkhano iyo, kuzindikira zamumtima uko, ndipo palibe wina angadziwe konse chomwe izo ziri, kupatula zitangokhala . . . Iwe umayenera kuti ubwere mu izo, kuti uzidziwe izo, mukuona. Palibe njira yoti uyesere kuzifotozoza izo. Palibe n—njira yomwe iwe ungakhazere kuchitira izo. Ndi chokuchitikira basi ch—chomwe palibe wina angadziwe, iwo okha omwe amapyola mu izo. Chomwe izo zimachita kwa mtundu wa anthu, chomwe izo zimachita kwa munthu, zimatulutsa moyo kuchokera mwa iye!

⁶ Chabwino, iwe umakhala mu maiko awiri. Iwe uli mu dziko *kuno*, ndipo iwe uli mu dziko *uko*, pamene iwe uli ndi winawake, mwina zaka fifite zapitazo; ndipo iwe ukhoza kukhala uli

ndi winawake, zaka kuyambira lero, zobwerazo; ndipo apobe iwe nkumazindikira kuti waima paguwa pano, ndipo iwe ukuyankhula chinachake chimene chinachitika zaka, zambiri mbiri kale; mwina masabata apitawo, miyezi yapitayo; fuko lina, malo ena, kapena chinachake. Ndiyeno iwe nkumayesera kudzisunga wekha mowongoka, mu izo, ndi kumaganiza; kudziuza iwe, ndi chinthu ndithu. Koma Ambuye atidalitsa ife mpaka pano, mu izo, ndipo ndife okondwa kwambiri, ndipo ndikudalira tsopano kuti Mulungu atenga ulemerero kuchokera mu msonkhanowu.

⁷ Tsopano, mu—misonkhano usikuuno, ine ndinaganiza, pomwe ife tangokhala anthu okwana mdzanja okha, palimodzi, misonkhano yathu imangolengezedwa komwe kuno, ndipo ndi ya anthu a kuno okha. Ndipo ife tisanalowe mu gawo lalikulu la misonkhano, ine ndinali kuganiza, lero, kuti ine ndikanayesera mwina kutenga zina za kuphunzitsa kwa kachitidwe-kachikale, kuchokera mu Baibulo, kukupereka kwa anthu; kuti pamene chochitika chachikuluchi chibwera, ngati Mulungu ati atumizire icho ife, ndiye ife tikhala omakhoza kumazimvetisa izo bwinoko.

⁸ Pambuyo pa zonse, machiritso Auzimu angokhala—nyambo pa mbeza, kuti ugwire nsomba, monga inu mukudziwa. Iyo imangokhala yomwe...Nsomba imagwira pa nyamboyo ndi kutenga mbeza. Chotero chachikulu chatu...Chodalira chatu chimodzi ndi ichi, kuti, miyoyo ipindulidwire kwa Yesu Khristu.

⁹ Ngati Mulungu akanakuchizani inu usikuuno, inu mukanakhoza kudzadwala kachiwiri inu musanafe. Inu mukhoza kudzadwala kachiwiri, mu chaka kuyambira tsopano, kapena zaka ziwiri kuchokera pano; mwina kudwala mu sabata kuyambira tsopano, kapena tsiku kuchokera pano. Ine sindikudziwa. Koma pali chinthu chimodzi chotsimikizika, inu mudzachoka pa dziko lino, ena a masiku awa, chifukwa ili langokhala la zigamba.

¹⁰ Koma moyo uwo ukangokhudzana ndi Mzimu Woyera ndi kubadwa kachiwiri, iwe uli nawo Moyo Wamuyaya. Ziribe kanthu zomwe ziti zichitike kuno, iwe sungawonongeke konse. Yesu anati, “Iye amene amva Mawu Anga, nakhulupirira pa Iye yemwe anandituma Ine, ali nawo,” iyo ndi tensi ya pakali pano, “Moyo wosatha, sadzabwera ku chiweruzo; koma ali,” tensi yakale, “wodutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo.” Izo zingatipangitse ife tonse Amethodisti ndi kuyamba kufuula, (si choncho izo?) ndiko kulondola, kuti ulingalire kuti, kuti Mulungu anachita izo. Tsopano, awo si mawu anga; awo ndi Ake, Yohane Woyera 5:24.

¹¹ Yohane Woyera 6, Yesu anati, “Iye amene adya thupi Langa, ndi kumwa Magazi Anga, ali nawo Moyo wosatha; ndipo Ine ndidzamuukitsa iye pa tsiku lotsiriza.” Ndiko kulondola. “Iye amene adya thupi Langa, ndi kumwa magazi Anga, ali nao,”

ndiyo tensi yatsopano, “Moyo wosatha.” Tsopano, “wosatha” uwu, iwo sumangopita kuchokera pa chitsitsimitso chimodzi kupita ku chimzake, koma umapita kudutsa mu Muyaya wonse.

¹² Ndipo tsopano, kwa atumiki ena inu omwe mwakhala, pafupi, mukudziwa kuti “Moyo” wosatha uwo umabwera kuchokera ku mawu omwewo omwe amatanthauza “Moyo wa Mulungu.” Mawu oti *Zoe*, mawu Achigriki, omwe amatanthauza “Moyo wa Mulungu Womwe.”

¹³ Ndiye, ife timakhala mwana wamwamuna kapena wamkazi wa Mulungu, mphukira ya Mulungu, tiri ndi gawo la Moyo wa Mulungu mwa ife. Ife sitingakhoze konse kuwonongeka monga Mulungu sangakhoze kuwonongeka, ngati izo zikanayesa. Chotero, ife tiri nawo Moyo wosatha; ndipo tidzaukitsidwa mu tsiku lotsiriza. Si zodabwitsa izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Izo zingawapangitse Abaptisti, Amethodisti, kugwirana chanza ndi kumafuula. Sichoncho izo? Ndithudi zingatero. Ndiko kulondola.

¹⁴ Ndicho chinthu chabwino cha chipembedzo cha nthawi-yakale. Icho chimangomupangitsa aliynse kukhala limodzi ndi kumakondana wina ndi mzake. Ndithudi chimatero. Chimachotsa kusiyana konse panjira, chimapanga zolengedwa zatsopano. Icho chingamupange wa k—kotho ya tokisido, ndi wa ovololo, kuika mikono yawo mokumbatirana wina ndi mzake ndi kuti, “M’bale, inu zikukuyenderani bwanji?” Ndiko kulondola. Ndithudi zingatero. Icho chingamupange wa diresi ya silika, ndi wa ya kalico, kuika mikono mokumbatirana ndi kuti, “Mlongo, ine ndimakukondani inu.” Ndi chomwe icho chimachita. Ndithudi icho chimatero, chimangong’ambira pansu kusiyana. “Olemera kapena osauka, ndife tonse amodzi mwa Khristu Yesu.”

¹⁵ Lamlungu, ku kachisi, chomwe ine ndikuwona pali gulu lonse la anthu aku kachisi ali pano, ife tinali—ife tinali nalo—phunziro la Sande sukulu pa, “chiwombolo mwa magazazi.” Ndipo ine ndinamangirizika kwambiri mu izo, mpaka ine ndikumverera ngati ine ndikadali panobe mu dera lina kwinakwake, pa: *Chiombolo Mwa Magazi*.

¹⁶ Ndipo usikuuno, banja litachoka kale ndipo ndinabwera kuno molawirira, kuti ndidzafike pomvera utumiki wa nyimbo, ndi zina zotero, ine ndinali mu chipinda. Ndipo zimawoneka ngati...ine ndinayamba kuweringa mu Lemba, ndipo ine ndinapeza chinachake. Ine ndinaganiza. “Chabwino, ngati Ambuye alola, ine ndingoyankhula pa izo kanthawi pang’ono usikuuno.”

¹⁷ Ndicho *Chiombolo Mwa Magazi*, Lamlungu. Tsopano, usikuuno, ine ndikuti ndiyankhule pa *Chiwombolo Mwa Mphamvu*. Ndipo mawa usiku ine ndati ndiyankhule pa *Chiwombolo Mwa Umphumphu*, (ngati Mulungu alola, ndiko

kuti), *Mu Chisangalalo*. Mu Magazi, mu mphamvu, ndi mu chisangalalo; chiwombolo!

¹⁸ Ndipo kuti ndikokere izi kunja... Tsopano, anthu ambiri, monga masikolala abwino, ophunzira amadziwa kutulukiramo kwake ndi kupereka vumbulutso la mtundu uwu, mwinamwake, la *izi*, kapena *izo*, kapena kuponyerapo zina. Koma, ine, ndine mtundu wa amodzi awa a mtundu wa osaphunzira pano wa alaliki omwe... Chinthu chokha chomwe ine ndimadziwa kuchichita, kuti nditsimikize kuti ine ndiri pafupi ndi cholondola, mulimonse, ndi kupita ku mithunzi. Ngati ine ndikanayamba kumapita ku khoma, ndi kuwala ku mbali *iyi*, ine ndikanakhoza kudziwa chomwe, basi momwe ine ndimawonekera; ngati ine ndikanakhala chinyama cha miyendo-inai, kapena—kapena mbalame, kapena chomwe icho chinali, ngati ine ndiwona mtundu wa mthunzi umene ine ndikuwonetsera.

¹⁹ Tsopano, Chipangano Chakale chinali mthunzi wa Chipangano Chatsopano. Icho chinali chosawoneka bwino. Monga mwezi, kwa dzuwa; dzuwa likamawalira pa mwezi, umanyezimiritsa kuwala kwa dziko lapansi. Ndipo ine ndimangochikonda Chipangano Chakale! Icho changokhala chodzaza ndi mafanizo monga choncho, kapena, monga momwe izo zingakhoze kukhalira. Tsopano, changwirowi...

²⁰ Mu Genesis, pamene Mulungu anapanga—dzuwa, poyamba, mwezi kenako, kuti mwezi ndi dzuwa ziziimira Khristu ndi Mpingo. Basi monga dzuwa limatuluka mwa mphamvu yake ndi ulemerero; ndipo pamene ilo lilowa, ilo limanyezimiritsa kuwala kwake kwa mwezi, mu mdima, kuti uzipereka kuwala kwa dziko lapansi pamene dzuwa lalowa. Yesu, pamene Iye anachoka, Iye anapita ku Ulemerero ndipo ananyezimiritsa Kuwala Kwake mwakukubwezera kwa Mpingo; kuti aziwupatsa, Mpingo, Kuwala kwa Uthenga mpaka Iye abwerere, o, mai, ndiyeno iwo adzakwatirana. Izo zidzakhala zodabwitsa. Kudzakhala kuli Kuwala kumodzi kwakukulu kwa mwezi ndi... “Mwanawankhosa ndiye kuwala kwake uko.” Iwo sakuwona dzuwa aponso, mu Mzinda.

²¹ Tsopano mwa kuwonetseratu pang’ono, tiyeni tipite mmbuyo mu Eksodo. Ndipo ine ndikuyembekeza inu simutopa ndi ine poyankhula mu Eksodo.

²² Nthawi ina, mu mpingo wanga kuwoloka mtsinjewu, ine ndinalalikirira, ine ndikukhulupirira, pafupi chaka ndi miyezi sikisi, pa Yobu, usiku uliwonse. Iwo akabwerera; ine ndimangotenga kagawo kakang’ono ka Yobu, ndi, kumapitiriza, ife timakhoza kuzipangitsa izo kuyenderera mu Baibulo.

²³ Lemba lililonse limalumikizana palimodzi. Mulibe kutsutsana mu Mawu a Mulungu. Ayi, bwana. Chidutswa chirichonse, nchangwirowi! Bukhu lokha lomwe linayamba

lalembedwa lomwe liri lodzozedwa monga choncho, lomwe lingakhoze mwangwiro. . . Linalembedwa ndi olemba ochuluka, ndipo mazana ochuluka a zaka motalikirana; ndipo mmodzi aliyense wa iwo, mwa Mzimu Woyera kuyankhula, kulumikizana limodzi kumene. Ndicho chifukwa, pa mabuku onse owonjezera awa, Amaccabee ndi zinthu, izo sizigwirizana ndi Ili, chotero ine sindimawavomereza iwo. *Ili* ndi Mawu a Mulungu, kwa ine.

²⁴ Ndipo mkazi wina anandilembera ine kalata ndipo anati. . . ine ndinali kulalikira; Yobu ali pa mulu wa phulusa. Iye anati, “M’bale Branham, inu mwakhala muli naye, Yobu ali pa mulu wa phulusa mwa utali wokwanira, inu simukuganiza? Nkuti tiri pafupi masabata sikisi.” Anati, “Bwanji, kodi inu simumuchotsapo iye pa mulu wa phulutsalo?”

²⁵ Chabwino, ine ndinati, “Pamene Mzimu Woyera uti uleke kukankhira Mawu cha kumeneko, ine ndikulingalira ine ndidzangosiya kunena izo.” Koma pamene Iye akupitiriza kundiyankhulitsa ine za iye ali pa mulu wa phulusa, chabwino, ine ndingokhala kumene ndi izo; ndipo miyoyo ili kumapululumutsidwa.

²⁶ Chotero, monga mlaliki, anabwera ku mzinda. Iye analalikira, usiku umodzi, iye analalikira pa kulapa. Usiku wotsatira, iye analalikira pa kulapa. Usiku wotsatira, iye analalikira pa kulapa. Atatha pafupi mausiku anai kapena asanu, gulu la madikoni linakumana naye ndipo anati, “M’bale, kodi inu simungakhoze kulalikira china chirichonse kupatula kulapa?”

²⁷ Anati, “O, eya. Iwo onse alape kaye, poyamba, ndiye ine ndilalikira pa chinachakenso.” Chotero ndilo—ganizo labwino. Iwo, mmodzi aliyense, alape, ndiye ife tikhoza kulalikira pa chinachakenso. Chabwino.

²⁸ Kwa kuwonetseratu pang’ono tsopano, kwa iwo, kapena makamaka iwo omwe panalibe ku Kachisi Lamlungu mmawa. Ife tikufuna kuti tibwerere mmbuyo ku mutu wa 12. Koma ganizo lathu lamaziko usikuuno liri mu mutu wa 14, kuyambira ndi ndime ya 13 ya Eksodo. Tsopano, ife tinasiyira pa ndime ya 10, Lamlungu mmawa, pa “*chiwombolo mwa magari*.” Ochuluka nonse inu mukuidziwa nkhaniyo, ine ndikutsimikiza.

²⁹ Tsopano ife tikudziwa kuti ife tikhoza kukokera mmbuyo masamba a Bukhu ili, ndi kutembenuza masamba awa. Koma alipo Mmodzi yekha Yemwe angakhoze kutsegula Bukhu, uyo ndi Yesu Khristu.

³⁰ Yohane analiwona Bukhu. Ilo liri losindikizidwa. “Ndipo iye analira chifukwa kunalibe munthu Kumwamba yemwe akanakhoza kulitsegula Ilo, panalibe munthu pa dziko lapansi, panalibe munthu pansu pa dziko lapansi. Koma kunali Mwanawankhosa yemwe anali ataphedwa kuchokera ku maziko a dziko lapansi, anabwera nadzatenga Bukhu kuchokera

mdzanja lamanja la Iye yemwe anakhala pa Mpandowachifumu, ndipo anatsegula zisindikizo ndi—ndi kutsegula b—Bukhu, anamatula zisindikizo zakezo. Ndipo Iye anali woyenera, pakuti Iye anali ataphedwa kuchokera ku maziko a dziko lapansi.”

³¹ Tiyezi tiyankhule kwa Iye, usikuuno, ndipo timupemphe Iye kuti atsegulire Ilo kwa ife pakali pano.

³² Tsopano, Atate achifundo, okonda, ife tikudza kwa Inu, kuyankhula ndi Inu, poyamba, mu Dzina la Yesu. Tikupemphera tsopano, kuti, pamene ife taima pano, titaphimbidwa pansa pa denga ili, usikuuno, kumene nkuntho uwo ukukukuma kunjako, mvula ikupotokola ndi kuwomba, ife tiri othokoza kwambiri pokhala nayo nyumba ya Mulungu yoti tibweremo. Ndipo ndife othokoza kuti ilipo nsanja, pothawirapo; Inu munati, “Dzina la Ambuye ndi nsanja yamphamvu; olungama amathawirako ndipo amakhala otetezeka.” Ndife okondwa kwambiri kuti ife tikulidziwa Dzina la Ambuye, ndipo tabwera mu Ilo.

³³ Tsopano ife tikupemphera kuti Inu mutsegulire Mawu awa kwa ife, usikuuno, Atate. Mulole Mzimu Woyera ubwere ndipo ulowe mu Mawu. Mudule milomo ya wantchito wosauka wodzichepetsa uyu, ndi mitima ya awo omwe ati azimvetsera, ana Anu. Ndipo mulole Mzimu Woyera ungowatenga Mawu a Mulungu ndi kuwakhazikitsa Iwo mu mtima uliwonse, basi momwe Iwo akusowekera. Mutidalitse ife tsopano. Apangeni malingaliro athu mwatsopano, usikuuno, mu Mzimu Wanu. Tengani ulemberero kuchokera ku utumikiwu. Mupulumutse otaika. Muchiritse odwala. Muwabweretse Kwawo obwerera mmbuyo, Ambuye. Ndipo ife tikupatsani Inu matamando, pakuti ife tikupempha izi mu Lanu, Dzina la Mwana Wanu wokondedwa, Yesu. Amen.

³⁴ Tsopano tembenezirani ku ndime ya 10 ya mutu wa 12 wa Eksodo. Ife tinali kuwerenga, “*chiombolo mwa magari,*” momwe kuti Mulungu anali atadzozzeratu mwanawankhosa kuti apchedwe mu nyumba iliyonse, momwe zinaliri kuti sipamayenera kuti pakhale kanthu kotsalira.

³⁵ Ziweruzo zinali zikugwa, ndipo chiweruzo chotsiriza tsopano, chinali chitakonzeka kuti chigwe. Mulungu amati akwaniritse Mawu Ake, mpaka pa lemba. Ndipo ziweruzo zonse izo mmbuyo umo zinali chizindikiro changwiwo, kapena choimira changwiwo, cha ziweruzo zomwe zakonzeka kuti zigwe tsopano.

³⁶ Ndipo ngati inu mutazindikira, chiweruzo chisanagwe. Tsopano atumiki akhoza kusagwirizana nane pa izi, zomwe ziri zabwino bwino. Koma chiweruzo chisanayambe kugunda Igupto, Mulungu anamutumiza Israeli ku Gosheni. Iwo anali mu Gosheni, ndipo panalibe mliri unagwera pa iwo. Choimira changwiwo cha Mpingo kutengedwera kwina, mu chisautso, mwaona. Chabwino.

³⁷ Ndiye pa mliri wotsiriza umene unakantha dziko lapansi uko, kapena unakantha Igupto, unali imfa. Nonse inu owerenga Baibulo pano, mukuwadziwa maphunziro anu a Sande sukulu ndi zina zotero, munatengapo izi, mwinamwake, nthawi zochulukuka. Koma, imfa inali mdani wotsiriza yemwe anakantha Igupto.

³⁸ Ndipo mdani wotsiriza yemwe ati akanthe mpingo tsopano ndi imfa, kuyankhula mwauzimu. Iwo omwe sati amutsatire Khristu, mu—mu ubatizo wa Mzimu Woyera, mwauzimu aumapo ndi kufa; mipingo, inu mukhoza kuziwona izo tsopano. Pambuyo pa zitsitsimutso zambiri mbiri, zazikulu zochulukuka ndi alaliki atadutsa mu dzikoli, ndipo, panobe, mpingo uli, izo ndizo, kuyankhula mwandale za mpingo, uli kuipira ipira nthawizonse. Mamembala ake akumangokhala mulimonse momwe iwo akufunira, kumachita chirichonse chimene iwo akuchifuna, komabe, nkumadzitchula okha Akhristu, ndi kumati iwo ali bwino.

³⁹ Kuti ukhale *Mkhristu*, zimatanthauza kukhala “wonga-Khristu.” Osapita ku malo omwe iwe sukanafuna kukhala uli ngati Khristu akanabwera. Osanena kanthu komwe iwe sukanafuna kunena pamene Khristu abwera. Osamachita kanthu komwe iwe sumayenera kuti uzichita pamene Khristu abwera. Osamaganiza kanthu komwe sukanafuna kumaganiza pamene Khristu abwera. Sungani cholinga chanu chimodzi, mtima wanu utakhazikika pa Kalvare. Amen. “Kumayenda mu Kuwala, pamene Iye ali mu Kuwala, ndipo ife tiri nacho chiyanjano kwa wina ndi mzake, ndipo Magazi a Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, amatiyeretsa ife kwa zosalungama zonse. Ndiwo Amethodisti, Abaptisti, ndi tonse ife, palimodzi, kutipanga ife tonse amodzi mwa Iye.

⁴⁰ Tsopano, chotsiriza, chinthu chotsiriza chinali imfa. Ndipo imfa iyo isanadze, kunali chitetezero chinapangidwira kwa imfa iyo, kwa onse omwe ankafuna kuti aithawe iyo.

⁴¹ Ndipo kunali chitetezero chinapangidwa chisanachitike chiwonongeko choyamba, cha dziko la chigumula. Mulungu anali naye mlaliki wa chilungamo, Nowa, ndipo iye analalikira zaka handiredi twente, kuti anthu abwere mu chombo. Ndipo iwo omwe mwakufuna anakana kuti apite, panalibe kanthu kanatsalira koma chiweruzo.

⁴² Ndipo, lero, munthu yemwe akukana kuti aziyenda mu Kuwala kwa Khristu, inu mwakana chifundo, chotero palibe kanthu katsalira koma chiweruzo. Ndizo zonse. Pangokhala mbali ya kumanja ndi ya kumanzere, imodzi yokha yomwe inu mungakhoze kupitako. Ndipo inu mupange kusankha kwanu.

⁴³ Tsopano, ife tikuona, usanati—usanabwere usiku woopsya wawukuluwo, momwe Israeli analamuliridwa. Ndipo ife tatenga kale izo, za kupha mwanawankhosa.

44 Mulungu anali akuubweretsa mpingo Wake kuti ulowe mu eksodo, kuti awutulutse iwo mu Igupto, kukalowa mu dziko lolonjezedwa. Ine ndikuzikonda izo. Iwo anali akupita uko, kuti akalitenge dzikolo. Mulungu anawapatsa iwo dzikolo, ndipo komabe ilo linali lonse lozunguliridwa ndi zinyumba zazikulu, ndi mipanda. Ndi makoma kuzungulira Yeriko, magaleta ankakhoza kuthamanga mijaha kuzungulira pa iwo. Ndipo tangoganizani za izo, komabe, Mulungu anati, “Ine ndakupatsani inu ilo. Ndi lanu.” Koma iwo anali woti aliyeretse, aliyeretse ilo.

45 Ndipo ndi chomwe Mulungu wachita lero. Iye wakupatsani aliyense wa inu, yemwe akuufuna Iwo, ubatizo wa Mzimu Woyera. Koma inu muyenera kuti mulowemo, mukautenge Iwo, ndizo zonse; kumenyera kusiyana, ndi kugwetsera pansi makoma, ndi kuyambapo kupita umo ndi kukautenga Iwo.

46 Inu mukuti, “Abusa ati, ‘Iwo si wa ife lero.’” Muzingoyenda chitsogolo kupitirira izo. “Amayi ati, ‘Ine ndikuthamangitsa iwe kunyumba.’” Pitanibe modutsa izo. “Amunanga ati, ‘Ine ndikusiya iwe.’” Mupitebe kudutsa izo. Ndizo zonse. Muyenera kuti mupite ndi kukautenga Iwo! Ndizo zonse.

47 Machiritso auzimu ndi a aliyense wa inu. Aliyense wa inu mwakhala pano usikuuno, muli ndi khansara, vuto la mtima, chirichonse chomwe chiri, Mulungu wapereka lonjezo. Ndipo ilo ndi lanu, koma inu muyenera kuti mupite ndi kukalitenga ilo.

48 Tsopano inu mukuti, “Chabwino, ine basi sindikumverera bwino kwambiri.” Izo ziribe kanthu kochita ndi izo. Lonjezolo ndi lanu. Mulungu analipereka ilo kwa inu. Mungopita mkati momwemo ndi kukawapha Afilisti, kuyambira ku mbali imodzi mpaka ku imzake. Ndipo mukawatulutsemo Ahivi onse ndi—ndi Aamori, mukangowaphamo iwo. Zipitanibe umo, ndi kukalitenga ilo. Mulungu anati, “Ilo ndi lanu. Pitani mukalitenge ilo.”

49 Koma Iye sanati, “Tsopano, Ine ndipita, ndikawasesako iwo onse, ndi kudzakumangirani inu mizinda ina yabwino, ndi kudzakukhazikani inu pansu mu msewu wophweka.” Iye samachita mwanjira iyo.

50 Iye amalipereka ilo kwa inu, ndipo inu muli nacho chinachake choti muchichite. Iye ndi wabwino mokwanira kuti pakukupatsani inu dziko, anati Iye akanati adzakuthandizeni inu ndi kudzakhalana. Pitani, mukalitenge ilo!

51 Ndipo ngati inu mukudwala, usikuuno, olumala, akhungu, ogontha, osayankhula, chirichonse chomwe inu muli; pitani, mukalitenge ilo. Mulungu anati ilo ndi lanu. Ilo ndi cholandira chanu. Mulungu analipereka ilo kwa inu.

52 Iye anawauza iwo kuti Iye akanadzawapatsa iwo dziko ilo. Anatomiza Mngelo patsogolo pawo, kuti awasamalire pa ulendowo, kawabweretsa iwo ku malo kumene ilo linali.

53 Tayang'anani pa azondi aja pamene iwo anapita uko. Apa anabwera khumi a iwo, anati, "O, ife sitingakhoze kuchita izo. Ndi zosatheka. Bwanji, ndife asayansi, ndipo ife tachiyang'ana chinthucho mobwereza. Ndi zosatheka mwasayansi. Ife sitingakhoze kuchita izo."

54 Koma kunali anthu awiri, mmodzi wa iwo dzina lake Yoswa, ndipo winayo dzina lake Kalebu. Iwo sanali kuyang'ana ku zomwe mbali yasayansi inali. Iwo anali kuyang'ana ku zomwe Mulungu ananena. Anati, "Ife tikhoza kuchita izo." Ndipo nkulondola. Ndipo iwo anabweretsa umboni wina kuti ilo linali dziko labwino.

55 Ndine wokondwa kwambiri ndi umboni umenewo, (simuli inu?) kuti liripo Dziko labwino pamwamba pathupa basi! [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Ndipo ife tiri paulendo wathu, usikuuno. Aleluya! Chabwino.

56 Apa iwo anali, tsopano, chiwombolo chisanachitike kumene. Mulungu ankafuna ana a Israeli, kuti iwo akhale ali otetezedwa ndithu, kuti aphe mwanawankhosa uyu. Ndi kuika magazi pa mphutu, pamwamba pa chitseko, monga *chonchi*; ndi pa mtengo uliwonse.

57 Ndipo iwo anali oti alowemo ndi kumakadya mwanawankhosa uyu, chidutswa chirichonse cha iye; zindikirani, mwanawankhosa yense, osati gawo chabe la iye. Chidutswa chirichonse cha iye chinali choti chidyedwe.

58 Anthu ena amati, "Ine ndingotenga gawo *ili*, ndipo ine—ine ndikukhulupirira gawo *ili*." Koma inu muyenera kuti mutenge Izo zonse, chidutswa chirichonse cha Iye. Mukuti, "O, ine ndikukhulupirira Iye anatunduzidwa chifukwa cha zolakwa zathu, koma, 'ndi mikwingwirima Yake,' ine sindikudziwa za Izo." Ife tikufuna Iwo onse. Chidutswa chirichonse cha Iwo ndi choti chizidyedwa; onse a Iwo. Zina za a Iwo zimalimba, koma ife tiyenera kuti tizidya Iwo, mulimonse. Mulungu ananena chomwecho.

59 Zindikirani ndime ya 10 tsopano.

Ndipo inu mudza—inu musalole kanthu ka iyo katsalire mpaka...mmawa; ndipo iyo yomwe iti itsalire...mpaka mmawa...mudzaiwotche ndi moto.

60 Ndipo, tsopano, pasakhale ina ya iyo iti itsalire; chirichose. Tsopano, Iye anati, "Pamene inu muzidya iyo, musati muzidya iyo yayiwisi, kapena yosapsya, koma inu muyenera kumadya iyo yophikidwa bwino." Ndipo ine ndikuzikonda izo.

61 Anthu amayesa kudya Mawu a Mulungu, ndipo iwo amawadya Iwo ngati kuti Iwo ndi aawisi; amatafuna pa Iwo, ndi kumalavula za Iwo, ndi china chirichonse. Amati, "O, ine sindingakhoze basi kuwadya Iwo. Ine sindingakhoze kupirira ndi Iwo." Iwo sanaphikidwe nkupsya mokwanira. Ndizo zonse.

⁶² Iye anati, “Muiphike iyo ndi moto.” Moto umaimira Mzimu Woyera. Inu mumutengere Mulungu mu mtima mwanu, poyamba, ndipo Iye ukuphikirani inu Iwo. Ndiko kulondola. Kuwaphika Iwo, mwabwino, kukometsedwa, ndiye Iwo amakoma bwino.

⁶³ Tsopano, inu simungakhoze kumaima monga *chonchi*, kunja, kumati, “O, ine, ine sindikudziwa ngati Iwo uli wa ine, kapena ayi. Iwo akhoza kukhala a masiku ena anapitawo.” Mungotenga Mzimu Woyera, poyamba, ndipo muwone chomwe machiritso Auzimu akutanthauza kwa inu ndiye.

⁶⁴ Penyani chomwe chipembedzo chomvereredwa mu mtima chikutanthauza kwa inu ndiye, pamene inu muli nao Mzimu Woyera umu woti umuphike Mwanawankhosa pamene Iye akubwera. Ameni. Ndiko kulondola. Muphikeni Mwanawankhosa, poyamba. Ndipo inu muyenera kuti mukhale nao Moto kuti mumuphike Iye nawo. Iye ayenera kuti awotchedwe. O, mai, ndi pamene Iye amakhala bwino. Kumuotcha Iye, iwo umangowotcha zonse. . .

⁶⁵ Ine ndinali nditaima kuno, osati kale litali, cha pa ng’ango yaikulu, ndipo ine ndinazindikira momwe motowo unaliri wotentha, ndipo iwo ungangophika ndi kuphika ndi kuphika. Ndipo pamene iwo unakhala wotentha, d—dothi mu zitsulo, mu golide, lonse limabwera pamwamba, ndipo iwo amayangapo izo. Ndipo iwo amakhoza kuwutenthetsa motowo motentha pang’ono mu ng’anjoyo. Ndiyeno pamene izi ziwira mowonjeza, iwo amapeza zinthu zina zosiyana, pairaiti ndi zinthu, kuchokera mwa izo.

⁶⁶ Zoyamba kubwera pamwamba zinali dothi, zonga dothi ndi matope. Zotsatira kubwerapo zinali zonga ore, o, zinazake zosakhala zabwino; siliva woyenderera wina, ndi zinthu zonse izi, izo zimabwera pamwamba, ndipo amayangapo izo. Ankapita pansu, pansu pomwe, ndipo chinthu chotsiriza chomwe ankatenga mwa izo chinali pairaiti. Ndiye golide waopusa.

⁶⁷ Inu mukudziwa ziripo zinthu zochuluka mwa anthu zomwe amayesera kupusitsana nazo wina ndi mzake pamene uli Mkristu, kapena kumachita monga ali, mulimonse. Mwaona? Koma iwe ukangolola Mzimu Woyera kuti uwiritse chirichonse, utenge—utenge golide waopusa yense kumuchotsa mwa iwe, aponso.

⁶⁸ Golide waopusa, anthu ambiri amapita Kumadzulo ndipo iwo amakapezako izo zina, ndipo iwo amaganiza, o, iwo abowoleza mgodi wa golide. Iye amanyezimira bwinoko kuposa momwe golide amachitira. Koma iye ndi golide waopusa, amakhala alibe mtengo kwa iye.

⁶⁹ Ndipo tsopano iwo amaziphika izo, ndipo iwo anangoziyengula izo zonse, ndipo amangophika izo ndi kuziphika izo, mpaka iye atakhala golide wangwiwo,

atawiritsidwa mpaka osakhala kanthu kena koma magawo handiredi golide.

⁷⁰ Ndipo umo ndi momwe Mulungu amachitira mu Mpingo Wake, amatsanulira Mzimu Woyera pa Iwo, ndipo umaphikitsa mmenemo mpaka Iye ataponyera kunja za chidziko zonse, ndi kusiyana, ndipo kudzikonda, ndi zonse izi, mpaka Iye amangoziwiritsa izo mwa munthu aliyense yemwe angabwere kwa Iye. Amen.

⁷¹ Tsopano, ndiye, inu mukhoza kuidya iyo. Pano pali lingaliro lina lokongola pano, pa—pa ndime ya 11.

Ndipo chotero inu muziidyia iyo; ndi mwanu... (mvetserani kwa izi)... mchiuno mutamanga, ... (ine ndikuzikonda izo)... nsapato pa mapazi anu, ... ndodo mu dzanja lanu; ndipo inu muziidyia iyo mofulumira; iyo ndi paskha wa Ambuye.

⁷² Ine ndikuzikonda izo. Pamene inu muzikadya, mukakhale muli okonzekera kumapita. Ndiyo nkhani yake.

⁷³ Tiyeni titembenezire ku Aefeso, cha pa mutu wa 6 wa Aefeso, ndipo tiyang'ane umu zomwe Paulo ananena za kuukonzeketsera Mpingo; mutu wa 6 wa Aefeso, kuyambira pa ndime ya 14 ya mutu wa 6.

Muime chotero, mutadzimangira mchiuno mwanu ndi choonadi, ... mutavalanso chapachifuwa cha chilungamo;

... mapazi anu atavekedwa ndi makonzekeredwe a uthenga wa mtendere;

Ndipo pamwamba pa zinthu zonse, mutenge chishango cha chikhulupiriro, chimene mudzakhoza kuzimitsa nacho... mivi yamoto ya woipayo.

Ndipo mutengenso chisoti cha chipulumutso, ndi lupanga la Mzimu, lomwe liri mawu a Mulungu:

⁷⁴ Muoneni Paulo akumuveka munthu wopita ku nkondo, kuti azikaguba:

⁷⁵ Mulungu, pa chiyambi, pa kuombola kwa Israeli, Iye anati, “Tsopano inu muyenera kuti mukhale okonzekera kuti muziguba. Pamene inu muti mubwere pansu pa magazi, muvale nsapato zanu. Mutadzimangira mchiuno mwanu. Mutenge ndodo yanu mu dzanja lanu ndipo mukonzekere kuitanako.” Ine ndikuzikonda izo.

⁷⁶ Munthu tsopano, pamene iye abwera mwa Khristu, iye amavalanso nsapato zake za Uthenga, kuti azilalikira Uthenga; atavala chisoti cha chipulumutso; chapachifuwa cha chilungamo; atadzimangira mchiuno mwake. Apo...

⁷⁷ Kawirikawiri, mwa asilikari akale, pamene iwo ankavala zitetezero za ku nkondo izo, iwo anali ndi lamba wamkulu.

Iwo ankamangira izo palimodzi, kugwirizira mchiuno mwawo, zishango izi, kuti azipherera nazo mivi ya mdani. Ndi phunziro lenileni bwanji ilo liri kwa ife. Ndipo pamene—chiuno chiyamba kufooka, kulera, chishango, iwo ankamangitsa pa lamba wawoyo, kubweretsa izo molimba kachiwiri.

⁷⁸ Ndi chithunzi changwiro bwanji, lero, pamene iwe uyamba kumverera ngati ukulekerera, kapena Mdierekezi akuti, “Nzopanda ntchito.” Muzifikira apo ndi kumangitsa lambayo pang’ono pokha; muzisolola lupanga mogwiritsa pang’ono mu dzanja, ndi kupita patsogolo. Ine ndikuzikonda izo, kukhala wokonzekera kukaguba

⁷⁹ Munthu aliyense yemwe ankayenda pansi pa magazi awo, usiku umenewo, analamulidwa kuti akhale umo, asati atulukemo mpaka kulamulira kubwere, kuti aziyenda.

⁸⁰ Ndipo munthu aliyense yemwe wabadwa mwa Mzimu wa Mulungu, akabwera mwa Khristu, ali nawo Moyo wosatha; amavala chishango chake, chapachifuwa chake, amaima wokonzeka, ndipo amaletsedwa kuti achokemo mpaka kulamula koti aziyenda.

⁸¹ O, kodi si zodabwitsa izo? Kodi sindinu okondwa kuti zonsezo ndi zosamaliridwa, usikuuno, inu asilikari? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.]

⁸² Tinali naye wotsogolera nyimbo ku Kachisi, nyimbo yathu yotiimira inali:

Nkhondo ili mkati, O asilikari Achikhristu,
 Maso ndi maso kuyima pa perete,
 Zida zikunyezimira, nyota zikuwonekera,
 Zolondola ndi zolakwika zakumanizana lero;
 Nkhondo ili mkati, koma musati mutope,
 Mukhale amphamvu ndipo mu mphamvu Yake
 mugwiritse zolimba;
 Ngati Mulungu ali wa ife, mbendera Yake ili
 pamwamba pa ife
 Tiimba nyimbo ya mgonjetsi potsiriza.

⁸³ Ambiri a oyera akale awo anapita kumanda. Koma limodzi la masiku awa, kutali mu dziko latsopano, pamene iwo azidzabwera mu Dziko lolonjezedwa, mbendera ya mtanda idzakhala pa ife, ndipo ife tidzaimba nyimbo ya mgonjetsi. Pamene ife tidzakhala pa Mgonero wa Chikwati usiku umenewo, kuzungulira gome, gome lalikulu ilo, mwina lalitali mailosi handiredi sauzande, ndi oyera-otsukidwa Mmagazi atakhala mozungulira apo. Ine ndikufuna ndidzapite pa gomelo ndi kukagwirana chanza ndi mmodzi aliyense wa iwo, ameni, kumangofuula. Inu mukufuna mutandimva ine ndikufuula? Dikirani mpaka ine ndidzakafike uko; mudzandipenye ine. Sindine wamkulu mokwanira, apabe, kwa izi.

Koma, zindikirani, tiyeni tiziguba tsopano. Khalani okonzeka. Ife tikupita.

⁸⁴ Pano pali chithunzi chachisoni, ife tisanati tifike ku phunziro lathu lachizolowezi, lomwe likupezeka mu ndime ya 38 apo. Mvetserani.

Ndipo unyinji wosakanizikirana unapita uko ndi ziweto zawo . . .

⁸⁵ Apo ndi pamene Israeli anapanga kulakwitsa. Chauzimu chinali chitachitidwa. Anthu osatembenuka anatsatira chifukwa cha chauzimu, potsiriza zinawafikitsa iwo mu vuto. Ndipo mpaka mmusi, ife tizindikira pano, cha pa ndime ya 42 ndi ndime ya 43. Ambuye akuyankhula kwa Mose, ananena, kuti, “Osati aliyense koma iwo omwe anaperekedwa nsembe . . . akanakhoza kudya nsembeyo,” kani, “koma iwo omwe anali odulidwa. Osati alendo, osati akunja, palibe mmodzi woti adye iyo koma iwo omwe ali odulidwa.”

⁸⁶ Ndipo ndi chamanyazi bwanji chomwe ife tiri nacho lero, mu tsiku lino, abwenzi okondedwa; kuti pamene, mu mpingo, aliyense yemwe ali wa mu mpingo amadya mgonero. Ndipo uko ndi kulakwitsa. Iwo okha omwe ali owomboledwa, ndiwo onse omwe ali oyenera.

⁸⁷ Yesaya anayankhula ndipo anati, “Magome a Ambuye ali odzaza ndi masanzi.” Anati, “Ndani yemwe nditi ndimuphunzitse Chiphunzitso? Iwo omwe achotsedwa ku maere.” Anati, “Langizo liyenera likhale pa Langizo; mzere pa mzere; apa pang’ono, ndi apo pang’ono.” “Ndipo gwiritsani zolimba ku zomwe ziri zabwino.” Mulungu akuyankhula, podziwa kuti tsiku lomwe ife tiri kukhalamo, kuti mpingo ukanadzakhala uli wandale kwambiri, mpaka iwo uzidzaloleza chirichonse, anthu, kumabweramo; bola ngati anali nalo dzina lawo pa bukhu la mpingo, iwo amakhala mamembala, iwo amadya mgonero.

⁸⁸ Ndipo Baibulo linati, “Iye yemwe adya ndi kumwa iwo, mosayenera ali wolakwira thupilo ndi Magazi a Ambuye.”

Yohane Woyera, mutu wa 13, Yesu akuyankhula.

⁸⁹ Akorinto Wachiwiri mutu wa 11, Paulo anati, zaka mtsogolo, kuti, “Iye yemwe adya ndi kumwa izi, mosayenera, adzakhala wochimwira thupi ndi Magazi a Ambuye. Mulole munthu adziyese yekha,” iye akuti, “iye asanati atenge.” Ine ndikubwereza Lemba. Ndiko kulondola. “Iye yemwe adya ndi kumwa, mosayenera, amadya ndi kumwera chiwonongeko kwa iyemwini, posalizindikira thupi la Ambuye. Ndipo pa chifukwa cha ichi ambiri akudwala ndipo ali ofooka pakati pa inu, ndipo ambiri agona.” Khalani otsimikiza kuti mukuima moyenera ndi Mulungu.

⁹⁰ Apa izo ziri mwa mthunzi, kuti, osati wina koma wodulidwa! Zinalibe kanthu momwe iye analiri womvera, momwe iye amathandizira mochuluka mpingo wa Chiyuda; iye ankayenera kuti akhale wotembenuka, ankayenera kuti akhale wokhulupirira wodulidwa kwenikweni, iye asanati atenge mgonero, kapena kudya paskha. O, momwe ife tachokera pa mzere lero!

⁹¹ Tsopano tiyeni tipite mwamsanga, ndiye. Ndipo Mulungu anawatulutsa iwo usikuuno. Ife tikutsegula tsopano ku ndime ya 13 ya mutu wa 14.

⁹² Mulungu anawapatsa iwo Lawi la Moto kuti lizipita patsogolo pawo. Ine ndikuganiza iwo anali nacho chithunzi muno, usikuuno. Ndipo ine ndikunena izo ndi kulemekeza. Kwa lingaliro langa loonamtima, pamene ife tiri pano mu gulu lino usikuuno, ine ndikukhulupirira kuti Ilo liri ndi ife usikuuno. Lawi la Moto lomwelo limene linkawatsogolera ana a Israeli, likupita patsogolo pathu, likuchita zizindikiro zomwezo ndi zodabwitsa. Ndipo mphunzitsi aliyense pano, kapena sikolala wa Baibulo, akudziwa kuti Mngelo yemwe ankatsatira Israeli ndi kuwatsogolera iwo waku dziko lolonjewedwa, anali Mngelo wa Pangano, yemwe anali Yesu Khristu.

⁹³ Ndipo, lero, “Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse” akutsatira patsogolo pa gulu ili lomwe inu mukufuna kuti muzilitcha oyera-odzigudubuza, ngati inu mukufuna kutero. Chabwino. Kupitirira patsogolo, kutsogolera kuchokera ku chigonjetso kupita ku chigonjetso! Mulungu alemekezeke!

⁹⁴ Mu mafuko awo, mu masiku amenewo, iwo anali kunyozedwa ndi kudedwa ndi kukanidwa, ndi kusiyidwa ndi mafuko, ndi kutchedwa chirichonse.

⁹⁵ Ndi momwe izo ziri lero, ndi wokhulupirira woona. Inu, mu mipingo yanu, inu mukudziwa, pamene inu mutenga kuima ndi Khristu ndi kunena Choonadi, mpingo wonse umati, “Tayang’anani pa iye! Iye wasokonezeka malingaliro. Iye wachita misala.” Mwaona?

⁹⁶ Musati mupereke chidwi kwa izo. Zitsatiranibe. Ndinu nonse oti muli nazo zida tsopano. Ndipo Magazi akupita patsogolo pa inu; Mzimu Woyera ukukutsogolerani inu. Muzingosunthabe. Musati mupereke chidwi kwa zomwe wina akuuzani inu. Muziyang’ana molunjika ku Kalvare, ndipo muziguba chopitirira. Choimira chokongola!

⁹⁷ Tsopano, iwo anali atatuluka, kudutsa, ndipo anafika... Ndipo tsopano zindikirani, chiwombolo cha magazi chinawatulutsa iwo mu Igupto, tsopano iwo ankayenera kuti akhale ndi chinachake tsopano choti chiwatengere iwo kupita mu dzikolo. Tsopano iwo akungoyamba kumene. Iwo anali atatuluka, anali atadulidwa, anabwera pansu pa magazi, ndipo

ali pa kuguba. Tsopano iwo anafika ku chinachake. Iwo anali akupita uko, akudziwa kuti iwo anali atadutsa kuchokera ku imfa kupita ku moyo; akudziwa kuti iwo anali nawo Moyo Wamuyaya.

⁹⁸ Koma apa iwo ali, akubwera chokwera tsopano, ndipo zovuta zinayamba kuwuka. Apa panabwera ankhondo a Farao, akuwatsatira iwo, kuti awatenge iwo. Vuto linayambikamo.

⁹⁹ Mvetserani! “Mulungu ndi pothawirapo pathu ndi mphamvu zathu, thandizo lopezekeratu mu nthawi ya vuto.” O, ine ndikuyembekeza inu mukuziona izi. Mwaona? Ndi izi apa. Dziwani. . . Koma, mvetserani, ndime ya 13 tsopano.

Ndipo Mose anati kwa anthuwo, Musaope inu ayi, . . .

¹⁰⁰ Ine ndikuzikonda izo. Yesu atawuka kale kwa akufa, Mawu Ake anali mosalekeza, “Musawope ayi.”

¹⁰¹ Ndi lomwe liri vuto ndi Mpingo lero, ukuchita mantha kwa imfa kuti inu mulephera. Inu mungakhoze bwanji kulephera pomwe muli mwa Khristu? Inu simungakhoze kulephera. Inu muli nawo Moyo wosatha. Ziwanda zonse mu gehena sizingakhoze kukugwedezani inu. Inu muli nawo Moyo wosatha. Yesu ananena chomwecho. Chotero musati muziwopa za kulephera.

¹⁰² Inu mukuti, “Chabwino, ine ndikuopa ine ndingakhale wotentheka.” Ine kulibwino ndikhale wotentheka pang’ono kuposa kungokhala chete ndi kusamachita kanthu. Ine ndithudi ndikanatero. Munthu yemwe angati achite chinachake. . .

¹⁰³ Zinanenedwa za Ballard kuno, munthu yemwe anabwera kudzapeza ntchito kwa iye, ndipo iye anati, “Ulembe dzina lako apa.” Iye anatenga pensulo yake, kuti alembe. Iye anati, “Chirikuti chofutira chako?”

Anati, “Ine sindiri ayi. . . sindilakwitsa kanthu.”

Iye anati, “Ine sindingakhoze kukugwiritsa iwe ntchito; iwe sumachita kalikonse.”

¹⁰⁴ Ndiko kulondola. Iwe sumalakwitsa konse, iwe suli ayi—iwe suli kuchita kanthu. Tiyeni tizipita, M’bale. Galamuka ndi kumapita. Ine ndikumukonda Longfellow apo:

Musati mundiuze ine, mwa ziwerengero za
chisoni,

Moyo uli koma loto lopanda kanthu!

Ndipo moyo ndi wakufa umene umagona,

Ndipo zinthu siziri momwe izo zimawonekera.

Anati, inde, moyo ndi weniweni! Ndipo moyo
ndi chitsimikizo!

Ndipo manda sindiwo mapeto ake;

Iwe ndiwe fumbi, ku fumbi umabwerera,

Sanali kukamba za solo.

Tiyeni ife tigramuke ndi kumachita,
 Ndi mtima pa zolimbanira zirizonse;
 Usati ukhale ngati ng'ombe, yoyendetsedwa!
 Khala mgonjetsi!

¹⁰⁵ Musati muziyembekezera kuti anthu azikukakamizirani inu kwa Khristu. Imani monga mwamuna kapena dona, mulandireni Iye, ndipo ziyendani chamtsogolo mwa chigonjetso. Amen. Ndi chimene Mulungu akufuna, asilikali, olimbika, okonzeka. Inu mukhoza kukhala musali, kulemera mapaundi handiredi ndi faifi, koma mukhoza kukhalabe wathanzi, m'bale, ndi wodzaza ndi mphamvu, ngati inu mutangomulola Mulungu kuti akhale nayo njira Yake. Ine ndawonapo amuna omwe ankalemera mapaundi thuu handiredi, alibe aunzi ya mwamuna mwa iwo. Ndiko kulondola. Chabwino. Zindikirani.

*...Mose ananena kwa anthuwo, Musawope...ayi,
 imani mwabata, ndipo muwone chipulumutso cha
 Yehova,...*

¹⁰⁶ Ndizo zabwino. Muzingoguba chamtsogolo. Musati muwopsyezedwe ndi kalikonse. Ngati inu mwamulandira Khristu ngati Mpulumutsi wanu, zipitirirani

¹⁰⁷ "M'bale Branham, ine ndikufuna ubatizo wa Mzimu Woyera." Zipitirizani kuyenda. Musati muwope.

¹⁰⁸ Inu mukuti, "Ine ndikudwala tsopano, M'bale Branham. Ine sindingakhoze kupita patsogolo kwambiri." Musati mutope. Ziyendanibe mtsogolo; muwone chipulumutso cha Ambuye wathu! Mulandire izo. Muzingosunthira mtsogolo.

¹⁰⁹ "Kodi izo zikhala motani? Adotolo andikana ine." Tsopano, munthuyo wachita zopambana zomwe iye akanakhoza, koma Mulungu sanachite zopambana Zake panobe. Ndiko kulondola.

¹¹⁰ Mphindi chabe, mvetserani kwa iye tsopano. Chabwino.

*...Yehova, zomwe iye ati asonyeze kwa inu lero:
 pakuti Aigupto (amatsenga, choonadi-...oyambitsa
 mavuto)...*

¹¹¹ Mukuti, "M'bale Branham, ngati ine ndikanangosiya kusuta! Ngati ine ndikanangoyika pansu kumwa! Ngati ine ndikanangosiya kuba kwanga! Ngati ine ndikanangosiya kuchita kwanga izi, izo, ndi zinazo." Musati mutope. Ziyendani chamtsogolobe. Mulungu asalalira zina zonsezo.

¹¹² "Ngati ine ndikanadziwa kuti ndingakhoze kuchita izo, M'bale Branham, ine ndikanamulandira Khristu pakali pano." Inu musati mudandaule. Zisunthani. Muzingopitirira patsogolo. Inu muwona chipulumutso cha Ambuye!

*...pakuti Aigupto omwe inu mukuwaona lero, inu
 simudzawaona konse iwo kachiwiri kwanthawi zonse.
 (Ameni. Izo zikonzedwa, pakapita kanthawi.)*

Yehova akumenyerani inu, ndipo inu mudzakhala . . . gwirani bata lanu.

Ndipo Yehova anati kwa Mose, Chifukwa chiani iwe ukulirira kwa ine? yankhula kwa ana a Israeli, kuti iwo azipita mtsogolo: (Ine ndikuzikonda izo.)

113 Musati muyesere kunena, kuti, “Chabwino, ine ndinajowina mpingo, zaka khumi zapitazo, M’bale Branham. Ine ndakhala ndiri membala wabwino wokhulupirika.” Izo nzabwino; ine ndikuyamikira izo. Koma tiyeni tisunthire patsogolo, usikuuno. Mulungu akusunthira patsogolo. Anthu lero, pano, iwo amabwerera mmbuyo, iwo amati, “Chabwino, tsopano . . .”

114 Sayansi, zaka handiredi fifite zapitazo; uko kunali sayansi mu France, yomwe inkati, “Ngati munthu atati apite konse pa liwiro lowopsya la mailosi sate pa ora, kukokera kwa pansi kungamuchotse iye pa dziko lapansi, ndipo iye angakhale atapita.” Anha! Mailosi sate pa ora? Iye akupita pafupi mailosi sikisitini handiredi pa ora tsopano. Inu simumamva konse sayansi ikulozera mmbuyo kwa munthu ameneyo. Iye ankalondola mu tsiku lake, koma iwo akukhala mu tsiku lina. Ndiko kulondola.

115 Koma, ife azilaliki, o, ayi. “Machiritso Auzimu? Tsopano ndiroleni ine ndiwone chomwe—chomwe Moody Woyera, Finney, Knox, Calvin, ena a iwo ananena pa Izo.” Iwo onse ankalondola mu masiku awo. Koma ife tikusunthira patsogolo, tikupita mtsogolo. Ife tiri ndi chinachakenso.

116 Yesu anati, mu fanizo apo, la wofetsa, pamene wofetsa anapita ndipo anakafetsa mbewu. Ndipo wina . . . Mdani anabwera mmbuyo ndipo anadzafetsa mbewu zina mu tirigu. Iye anati, “Zisiyeni izo zikulire palimodzi.”

117 Inu nthawizonse mumaloza pa momwe dziko liri kukhalira loyipa, koma inu mukulephera kuti muwone momwe Mpingo ukukhalira wamphamvu, pa nthawi yomweyo. Iwo ukuwuka, ukuima mmundawu. Chomwe, Iwo uli gulu lapang’ono, koma, m’bale, Mulungu ali ndi Iwo. Ndipo Iwo ukupita mwachigonjetso motsimikiza basi monga Khristu anakira kwa akufa. Ameni. Mpingo wa Mulungu sudzalephera konse. “Zipata za gehena sizidzaugonjetsa Iwo.” Zikusonyeza kuti iwo azidzautsutsa Iwo, koma iwo sangakhoze kuugonjetsa. Mpingo ugonjetsa, kupyolera mu Magazi a Yesu Khristu, mpaka ku malo a chigonjetso. Ndine wotsimikiza pa chinthu chimodzi ichi, kuti Mulungu akhala nawo Mpingo wopanda banga, khwinya, kapena chilema. Ameni. Ndine wokondwa kwambiri nazo.

118 Tsopano, “Ngati ine ndiri mu Mpingo umenewo.” Ameni. “M’bale Branham, kodi iwe umalowa mwa Iwo chotani, ndi kalata?” Ayi. “Iwe umalowa chotani mwa Iwo?” Mwa Kubadwa; kubadwira mu Iwo!

119 Ine ndakhala ndiri mu banja la a Branham, zikhala ziri zaka forte-faifi, tsiku la sikisi la Epulo akubwera uyu, ndipo iwo sanachite kundifunsa konse ine kuti ndijowine banja lawo. Ine ndinabadwa ndiri Branham. Ine nthawizonse ndidzakhala ndiri Branham.

120 Ine ndinabadwa kukhala Mkhristu, mwa Yesu Khristu. Ine ndidzakhala ndiri Mkhristu, chifukwa Mulungu anadzozeratu izo chotero, mwa kusankha. Iye anatiyitana ife, kupyolera mu chisomo cha Mwana Wake Yemwe wokonedwa. Ife tinamulandira Iye ndipo tiri nawo Moyo Wamuyaya. “Mwa kugwirana chanza kumodzi”? “Mwa umembala umodzi”? “Mwa kalata imodzi”? “Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi, Yesu Khristu,” ndipo apo tinakhala mbadwa limodzi za Ufumu.

121 Ine ndinali kuganiza lero, pamene ine ndinali kutali ndikupemphera, kuti momwe ili liliri tsiku lomwe ife titi tidzakaliyankhire. Ine sindidasowa kuti ndidzakayankhire kwa m’badwo umene unalipo ine palibe, kapena m’badwo umene uti udzakhalepo ine nditachoka. Koma, mu Chiweruzo, ine ndi woti ndidzaimo nao m’badwo uno. Ndipo ine ndinati, “Tayang’anani apo, chithunzi cha mkazi pa chikwangwanicho, akumwamowa, chinachake chimzake, ndinati iye anali ‘wopanda mpweya,’ kapena chinachake.” Ine ndinati, “Inde, wopanda-Moyo, naponso.” Chabwino. Ndi zimenezo inu. Ine ndinati, “Ndi chamanyazi bwanji!”

122 “Pa kulalikira konseku,” ine ndinati, “nthawizina izo zimawoneka,” ine ndinamuza mkazi wanga, ine ndinati, “nthawizina izo zimawoneka kuti izo sizikuchitira ubwino uliwonse. Koma ine ndiyenera kuti ndikhale liwu lochenjeza, mulimonse, mosasamala zomwe anthu akuchita nazo. Ine ndiyenera kuti ndizilalikira Uthenga, mulimonse, ndi kuperekera umboni kwa chiukitsiro ndi Mphamvu ya Yesu Khristu.” Asiyeni iwo akane Izo, ndi kutembenezira msana wawo mmbuyo; Mulungu adzawaweruzo iwo pa Chiweruzo chifukwa cha izo. Ine ndiri nawo udindo pa kulalikira kokha, ndi azitumiki ena nawonso, omwe amalalikira Uthenga.

123 Tsopano, ine ndikungozikonda Izi. Zindikirani, “Pitani patsogolo tsopano,” ndipo inu muwona ulemerero wa Mulungu. Koma, mveterani, ndime ya 16 tsopano. Ife tikuwerenga izi.

Koma kwezera . . . mmwamba ndodo, . . .

124 “Ndodo,” iyo inali ndodo yachiweruzo. Tsopano, iyo siinali ndodo ya Mose. Iyo inali ndodo ya Mulungu. Ngati inu mungazindikire, Mose, iye amaitenga ndodo iyo, iye akailozetsa iyo mmwamba monga *chonchi*, utitiri umabwera. Iye akailozetsa iyo pa madzi, iwo amasandulika magazi. Iyo inali ndodo ya chiweruzo cha Mulungu. Ndipo ndodo yomweyo . . . Mvetsani izo! Ndodo yomweyo inali yomwe iye anakanthira nayo

thanthwe; ndipo mng'aru unabwera mmbali mwa thanthwe, ndipo madzi unabwera kuchokera mu thanthwelo.

¹²⁵ Tsopano, thanthwe ilo linali Khristu, ndipo icho chinali chiweruzo cha Mulungu. “Tsiku limene inu mudzadya icho, tsiku limenelo inu mudzafa.” Anamukantha Khristu pa Kalvare, ndipo analipira imfa yowawa, yopweteketsa ija. Palibe munthu, akanakhoza konse kufotokoza chomwe icho chinali, kapena sadzakhalapo konse. Apo Mulungu anaika chiweruzo chonse Chaumulungu pa Iye, ndipo anamukantha Iye mmbali, pamene kuchokera mmbali Mwake munatuluka madzi ndi Magazi ndi Mzimu, kwa chiombolo chathu.

¹²⁶ Momwe anthu amajambulira chithunzi Chake, nthawizina, ali ndi mkanjo momuzengeza Iye, kapena chinachake chimzake, pa mtanda. Izo siziri chomwecho. Iwo anamuvula Munthu uyo, moipa mulimonse, chinthu chonyansa chimene iwo akanakhoza; koma Iye akanayenera kuti akhale. Apo Iye anali, wapamwamba ndi wokhulupirikitsitsa wa mdziko lonse, yemwe anayamba wakhalapo kapena ati adzakhalepo. Ndiyeno anavulidwa, maliseche pa mtanda; anavulazidwa, anakanthidwa, akuukha magazi; khololo lolavuliridwa mwa mnyozo likulendewera pa nkhope Yake; chisoti cha chitonzo cha minga pa mutu Wake. Koma apo ndi pamene Iye anagonjetsa imfa, hade, tchimo, matenda, ndi manda, ndipo analipirira mtengo wa ife tonse.

¹²⁷ Izo zimanenedwa kawirikawiri, nthawizina, “Apo ndi pamene Iye anachotsa mbola ya imfa.” Ndi pamene Paulo anati, “O imfa, mbola yako ili kuti?”

¹²⁸ Ine ndauidwa kuti ziwala zambiri, njuchi ndi zinthu, izo ziri ndi mbola, ndipo izo ziri ndi chiphe, mwa izo. Koma nthawi imodzi izo zikaluma, izo zimataya mbola zawo.

¹²⁹ Imfa inali nayo mbola mwa iyo, nthawi ina; koma Khristu, pa Kalvare, anachotsa mbola kwa imfa. Aleluya! O, pamene ine ndiganiza za izo! Apo Iye anasolola mbola kwa imfayo, chifukwa cha ine ndi inu, mbola yonse ya imfa.

¹³⁰ Paulo anati, pamene iwo ankapita kuti akadule mutu wake, mu ndende ya Chiroma, iye anati, “Imfa, mbola yako ili kuti?” Analozera mmbuyo ku Kalvare, ndipo uko ndi komwe mbola inachotsedwa pa imfa. “Manda, chigonjetso chako chiri kuti?” Iye anati, “Koma mathokozo akhale kwa Mulungu, izo zikutipatsa ife chigonjetso kupyolera mwa Ambuye wathu Yesu Khristu.” Ameni. Chabwino.

...ndodo (chiweruzo), ndipo uitambasulire iyo apo... uphimbe n—nyanja, ndipo uigawanize iyo: ndipo ana a Israeli adutsa pa nthaka youma kudutsa pakati pa nyanja.

Ndipo ine, taonani ndiumitsa mtima wa Aigupto, ndipo iwo akutsatirani inu: ndipo ine ndidzazipezera

kulemekezedwa pa Farao, ndi pa khamu lake lonse, ndi pa agareta, ndi pa aamuna apa kavalo.

Ndipo Aigupto adzadziwa kuti Ine ndine Yehova, ndipo ine ndadzitengera ulemu pa Farao, ndi pa agareta ake, ndi pa akavalo ake.

Ndipo mngelo wa Mulungu, . . .

¹³¹ Mvetserani! Mangitsani chishyalo tsopano. “Ndipo Mngelo wa Mulungu, yemwe ankapita patsogolo pa msasa wa Israeli,” Iye akadali yemweyo.

. . . mngelo wa Mulungu, yemwe anapita patsogolo pa msasa wa Israeli, anachoka ndipo anapita mmbuyo mwa iwo; ndi lawi la mtambo linachoka patsogolo pa nkhope zawo, ndipo linadzaima kumbuyo kwawo: (kapena, linapita kuchokera apa, ndipo linakaima kumbuyo uku; mkhala-pakati mu nthawi ya vuto.)

¹³² Pamene vuto liyamba kukomana nanu, matenda pa dzanja lililonse, vuto, Mngelo wa Mulungu amabwerapo, amapita pakati pa inu ndi matenda, ndipo amadzaima apo mu njira, kukutsutsani inu kuti mutenge Mawu a Mulungu.

¹³³ Mulungu anali atamupatsa Israeli lonjezo, kuti iwo anali kupita mu dzikolo. Uko kunali mamilioni, mwinamwake, a anthu, akubwera, kuti awatsatire iwo ndi kuwathamangitsa iwo, ndi kuwadulira iwo pansu, monga gulu la zinyama. Koma Mngelo wa Ambuye, Yemwe anali uko kuti awatengere iwo ku dziko lolonjezedwa, anauka kuchokera mu msasa ndipo anapita nakaima pakati pa iwo ndi chowopsyacho.

¹³⁴ Aleluya! Iye akuchitabe izo. Iye adzapanga njira. O, ine ndikungomukonda Iye chifukwa cha izo, sichoncho inu? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.] Iye amupangira njira munthu wodwala aliyense yemwe wakhala muno pakali pano. Iye anapanga kale njira, ndipo Iye akuima pakati pa inu ndi vuto.

¹³⁵ Ndipo ine ndikudziwa Iye ali muno pakali pano. Inu mukhoza kumanditcha ine wotentheka ngati inu mukufuna kutero; ine ndiribe choyankhira pa zomwe inu munena. Koma ine ndiri ndi choyankhira pa zomwe ine ndikunena, pamaso pa Mulungu. Koma Iye Yemwe anawatsogolera ana a Israeli, ngati ine ndaweruza izo molondola, pa Kuwala uko komwe inu mukukuwona usikuuno, kapena munakuwona pa chithunzi chija. Ine ndikuganiza iwo aziyika muno izo usikuuno. Mngelo yemwe uja wa Mulungu ali mu nyumba ino pakali pano, kuti achite ndendende basi zomwe Yesu ankazichita mu tsiku lija. Iye ali pano kuti atsimikizire. Basi zomwe Iye ankachita apo, Iye ali tsopano, ndipo akhala nthawizonse ali yemweyo. Mngelo wa Mulungu, akusuntha chokwera kuti aime pakati pa ife ndi matenda, aime pakati pa ife ndi imfa.

¹³⁶ Palibe zodabwitsa Davide anati, “Eya, ngakhale ine ndiyenda kupyola mchigwa cha mthunzi wa imfa, ine sindidzawopa choipa: chifukwa Inu muli ndi ine.” Ndithudi.

¹³⁷ Ataima apo, Mngelo wa Mulungu anapita patsogolo pa msasa wa Israeli, ndipo anasuntha, ndipo anapita nakaima pakati pa iwo ndi adani.

¹³⁸ Ndipo Mngelo wa Mulungu waima, usikuuno, pakati pa aliyense payekha pano ndi mdani. Ine ndikudziwa zomwe ine ndikuzikamba. Ine ndikudziwa, pomwe ine ndaima pano tsopano pa nsanjapa, pamaso pa gulu laling’ono ili usikuuno, ine ndikudziwa kuti Mulungu watsika, wabwera pansi kuchokera ku Ulemerero, ndipo waima mu nyumba ino tsopano. Ngati inu muti mungoyerekeza kuti musunthire pa Mawu a Mulungu, muwone ngati Iye sasunthira pamaso panu. Penyani.

¹³⁹ Ndipo Ilo linabwera pakati pa msasa ndi Aigupto. Iye akubwera pakati pa inu ndi matenda anu. Iye waima pakati pa inu ndi machimo anu, pakali pano. Chifukwa? Ife tiri mu eksodo wa Mpingo. Igupto anali nthawizonse kutchedwa dziko, ndipo pamene Israeli anabwera kuchokera . . . Kumbukirani, iwo anali mamembala a mpingo kumeneko. Koma magazi ndi chitetezero zitapangidwa kale, iwo anakhala odulidwa a Mulungu.

¹⁴⁰ Ndipo mdulidwe, lero, ndi ubatizo wa Mzimu Woyera. “Nonse,” anatero Stefano, “nonse inu osadulidwa mu mtima ndi makutu, nchifukwa chiani inu nthawizonse mumaukaniza Mzimu Woyera? Monga makolo anu ankachita, chomwechonso inu.” Mzimu Woyera umadula mu mtima, kudula nkuzichotsa zinthu za mdziko. Poyamba unali mpingo wa chiyero cha kachitidwe-kachikale unkakhala moyo umenewo, unkachita monga choncho, unkakhala moyo monga iwo. Koma, lero, zangokhala chimodzimodzi monga dziko lonse. Ndi chamanyazi. Ife talekerera zigwiriro.

¹⁴¹ M’bale wokalamba Spurgeon anakonda kunena kuti, mlaliki wakale wachi Methodist bwenzi wanga, anakonda kuimba nyimbo.

Ife talekerera zigwiriro, talekerera zigwiriro,
Ife tanyengerera pa tchimo.
Ife talekerera zigwiriro, nkhosa zatulukamo.
Kodi mbuzi zalowamo chotani?

¹⁴² Chifukwa inu mwalekerera zigwiriro! Ndi choncho. Inu mwalekerera muyezo wa chikhalidwe cha Chikhristu, chifukwa maseminare aswa alaliki angapo ndipo awatumiza iwo kunja kuti azikanyengerera ndi Choonadi. Koma Mzimu Woyera nthawizonse wakhala ulipo kuti uzitsutsa tchimo, ndipo ulipo usikuuno kuima pakati pa wokhulupirira ndi zinthu za mdziko. Amen.

Ndipo iwo unabwera pakati pa msasa wa Aigupto ndi msasa wa Israeli; ndipo iwo unali mtambo wa mdima

kwa iwo, koma iwo unkapereka kuwala mu usiku kwa awa: chotero kuti enawo sankayandikira anzawowo usiku wonse.

143 Penyani, chinthu chomwecho chomwe chinaperekedwa kwa gulu *ili* la okhulupirira, Kuwala, kunali kuwachititsa *awo* khungu.

144 Chabwino, valani zikhoto zanu zosadutsa-nyese. Ndi izi zikubwerazi. Penyani, munthu aliyense yemwe akana Kuwala amachita khungu ndipo amayenda mu mdima chifukwa inu simukukulandira Kuwala. Ameni. Mulungu amatumiza atumiki omwe amalalikira Uthenga. Iye amatumiza zizindikiro ndi zodabwitsa pakati pa anthu, kuti awatsimikiritse Iwo kuti ndi Choonadi; ndipo anthu amawukana Iwo, palibe kanthu katsalira koma mdima kwa inu. Ziyendani mu Kuwala pamene Kuwala kuli kuwala, m'bale wanga. Kulandireni Kuwala. Khristu ndiye Kuwala. Iye wabwera kuti abweretse Kuwala kwa inu. Koma iwo omwe anakukana Kuwala analandira mdima. Ndipo mwamuna aliyense ndi mkazi, usikuuno, yemwe akukana Kuwala, akuyenda mu mdima, osadziwa kumene iye akupita. Iye akuzandima akutsatira bwino kwambiri, yotchuka ndi anthu, koma ndikudabwa momwe akuimira Pamaso pa Mulungu.

145 Zindikirani izi! Chinthu chodabwitsa chake pano. Iye anali Kuwala kwa amodzi, ndi mdima kwa enawo. Aisraeli, ndiye, Mose atapemphera kale, iwo akanakhoza kugona pansu mwa mtendere. Tsopano penyani.

Ndipo Mose anatambasulira dzanja lake pa nyanja; ndipo Yehova anapangitsa nyanja kubwerera mmbuyo ndi mphepo yamphamvu ya kummawa usiku wonse uwo, ndipo anapangitsa nyanja mtunda wouma, ndipo madzi anagawikana.

Ndipo ana a Israeli anapita mpaka pakati pa nyanja pa nthaka youma: . . .

146 Ngati inu mungazindikire, pamene ana a Israeli, omwe anali atabwera kuchokera mu mdima ndipo anakulandira Kuwala, pamene iwo anafika mu vuto, Kuwala kunatembenukira mmbuyo mozungulira. Ndipo iwo anagona usiku wonse. Ndipo pamene iwo anali akugona, Mulungu anali kutumiza mphepo, kumawomba kudutsa pa nyanjayo, kutsegula njira yothawirapo.

147 Aleluya kwa Mwanawankhosa! Ndine wokondwa kwambiri kuti ine ndadzazidwa ndi Mzimu Woyera, usikuuno. Pamene ife tiri kugona, kusangalala, kupumula mu lonjezo la Mulungu!

148 Mulungu anawalonjeza iwo, kuti apanga njira yothawirapo. Ndipo pamene iwo anali kupumula pa lonjezo ili, Mulungu anali kumeneko, patsogolo pa iwo, akutsegula njira.

149 Mwamuna aliyense ndi mkazi, usikuuno, yemwe ati amuvomereze Yesu Khristu pa maziko awo; Mzimu Woyera,

pamene inu muli chigonere, pamene inu muli kupumula mu lonjezo Lake. Mwina ndinu wopuwala; mwina ndinu wakhungu; mwina inu simukukhoza kumva; mwina inu simukukhoza kuwona; mwina inu mukudwala; vuto la mtima, khansara, kapena chinachake, mukufa. Kulandireni Kuwala, usikuuno, ndipo mupumule pa Iko.

¹⁵⁰ Ndipo mphepo, ikubwera ngati mkokomo wa mphepo yamphamvu pa Tsiku la Pentekoste, isunthira apo ndi kukutsegulirani inu njira, alaluya, kuti inu mudutse apo pomwe mu chigwa icho cha matenda, kubwerera kumene mpaka mu dziko la thanzi kachiwiri. Inu mudutsa kumene mu dziko lozizira ilo, lofunda, lomangidwa-unyolo, zipembedzo zosayanjanika; kukhala a mtima wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, wokondwa, wosangalala, wodzaza ndi chisangalalo.

¹⁵¹ Mulungu amasonyeza mphamvu Yake, ndipo anali kuisonyeza iyo. Mundikhululukire ine, ine ndayamba kufuula kwambiri. Kusonyeza chiwombolo mwa mphamvu. Iye anasonyeza magazi kumbuyo uko, pa chinthu chimodzi. Iye anasonyeza mphamvu Yake kuno, mwa Magazi Ake, kupyolera mu chiwombolo. Anasonyeza mphamvu Yake kuti tithawe imfa, kupyolera mu magazi. Iye anasonyeza mphamvu Yake kuti apange njira yothawirapo, mwa kuwombola kwa mphamvu.

¹⁵² Ndipo, lero, inu amene mwawalandira, ameni, inu amene mwalandira Magazi a Yesu Khristu, kuti akutsukeni inu kwa tchimo, mphamvu ya Mzimu Woyera ili pano kuti ikutsogolereni inu ku ubatizo wa Mzimu Woyera. Mphamvu ya Mulungu ili pano kuti ikusintheni inu kuchokera ku matenda kupita ku thanzi. Mulungu, akusuntha chamtsogolo, mu eksodo ya Mpingo Wake! Iye akubwera mu chifuwa, kumene Mulungu ati akasonkhanitse, pakapita kanthawi, mbewa Yake. Zodabwitsa, kubwera kuchokera ku mdima, kupita mu Kuwala kodabwitsa! Momwe ife tikuzikondera izo! Momwe ine ndikuchitira! Chomwe izo zikutanthauza kwa solo yanga, usikuuno! Abwenzi, inu. . .

¹⁵³ Ine ndinali kuyankhula kwa bambo lero, yemwe anangokomana nane pamene ine ndinali panja. Ndipo iye anati, “Ine ndakhala ndikuyesera kuwauza anthu.” Anati, “Ine ndasintha kwambiri, Billy, kuyambira pamene iwe unali mwana.” Anati, “Iwe unakonda kudzerako ndi kumandiuza ine, ku malo anga amalonda, kuti ine ndiyenera kuti ndikonze bwino ndi Mulungu, ine ndiyenera kuti ndiyanjane naye Mulungu.” Ndipo anati, “ine ndinkakhala ngati ndinkaseka pa iwe. Koma,” anati, “Billy, zinthu zasintha tsopano.” Anati, “ine ndikudziwa tsopano zomwe iwe ukuzinenazo.”

Ine ndinaganiza, “Mulungu alemekezeke!”

¹⁵⁴ Iye anati, “Ine ndikuyesera kuwauza ena za izo,” ndipo anati, “iwo amasintha phunzirolo ndipo amamka namayankhula

za pepala yachilendo kapena chinachake. O, izo si za ine ayi. Munthu wotsatira uyu pa ngodya, iye akhoza kufa. Iye ndi wotsatira wina. Mwina nambala yake ndi yotsatira, posadziwa kuti nambala yotsatira ndi ya ndani.” Iyo ikhoza kukhala ili yanu, usikuuno, abwenzi. Iyi ikhoza kukhala nthawi yomwe Mulungu akukuitanani inu.

¹⁵⁵ Mulungu, Mzimu Woyera waukulu, waima pano usikuuno, pakati pa imfa ndi Moyo; waima pano usikuuno, pakati pa matenda ndi thanzi. Ine ndikudziwa chomwe ine ndikuchikamba. Ndiko kulondola. Pakali pano, Mzimu Woyera womwewe umene inu mukuumverera tsopano, munthu aliyense wobadwa-kachiwiri ali woti awumverera Mzimu uwo mu chipindamu. Inu simungakhoze kuziletsa izo. Ngati inu muli nawo Moyo uliwonse, inu mukudziwa kuti Iwo ulipo. Chabwino.

¹⁵⁶ Momwe monga maginito, pamene iwo. . . Pamene maginito aakulu abwera pafupi ndi zinthu, izo zimayamba kusuntha ndi kumakwawa, (chifukwa?) zikamafika pafupi. Monga maginito aakulu anabwera pansi, mmwamba kuno, nthawi ina, ku Hammond, Indiana. Ine ndinali kuwawona iwo akutola zodulidwa, pansi. Iwo anakoka chiwongolero chachikulu kwambiri; pansi pankabwera maginito aakulu. Ndipo iwo anali ndi zodulidwa zonse zitasesedwa pakati pa bwalolo. Ndipo pamene icho chinkadutsa apo, zodulidwa zonse izo zomwe zinali ndi nyese kwa maginito, zitsulo, zinapita mmwamba momwe ndipo zinapita ndi maginito, kunjja. Ndipo iwo anachotsa maginito kwa izo, anazigwetsera izo mu chimphika, ndipo ankaziwumba izo kachiwiri. Apo panali zodulidwa zambiri za aluminiamu zinatsalira. Ine ndinati, “Nchifukwa chiani izo sizinapite?”

Iye anati, “Izo ziribe nyese kwa maginito.”

¹⁵⁷ Ine ndinati, “Mulungu alemekezeke.” Ine ndinati, “Nchifukwa chiani izi sizinapite, pansi apa, chidutswa cha chitsulo ichi?”

Anati, “Ngati inu mukanazindikira, icho chamangiriridwa pansi.”

¹⁵⁸ Ndipo izo ndi zonga anthu ochuluka usikuuno, abwenzi. Inu mwakhala membala wa mpingo, koma opanda nyese mwa Mzimu Woyera. Ndiye inu mukulola zina kuti zikumangireni inu pansi, kusiyana kwina, kukumangirireni inu pansi.

¹⁵⁹ Koma limodzi la masiku awa, pakhala maginito aakulu ati abwere kuchokera Kummawa, otchedwa Mwana wa Mulungu, omwe ati adzasese dziko lino. Ndipo munthu aliyense yemwe ali wakufa mwa Khristu adzauka ndi Iye, kuti apite kutaliko. Ndipo matupi okalamba awa adzasinthidwa ndi kupangidwa mwa mawonekedwe Ake, monga mwa thupi Lake Lomwe laulemerero, komwe ife titi tidzakakhale moyo kwanthawi zanthawi, afulu ku matenda, afulu ku ukalamba,

afulu kwa chinthu chirichonse; ndipo mu Ulemerero wa Mulungu, kukakhala moyo mu Kukhalapo Kwake kodala kwa nthawizonse. Amen. Musati mulole izo zikuwopsyezeni inu. Ine ndikumverera mwachipembedzo pakali pano. Ine ndithudi ndikutero. Chabwino.

¹⁶⁰ “Pakuti ine ndikudziwa kuti muomboli wanga ali moyo, ndipo pa masiku otsiriza Iye adzaima pa dziko lapansi lino; ngakhale nyongolosi za khungu zitaliwononga thupi ili, komabe mu thupi langa ine ndidzamuwona Mulungu; yemwe ine nditi ndidzamuwone mwa ndekha; maso anga adzamuwona, ndipo osati a wina.”

¹⁶¹ Musati muganize kuti ine ndapenga. Ine sindiri. Ngati ine ndiri, mungondisiya ine ndekha. Ndine wokondwa kwambiri mwanjira iyi kuposa momwe ine ndinaliri mwa njira inayo. Inde, bwana. Mungondisiya ine ndizikhala mwanjira iyi. O, zedi, “wopenga,” kwa dziko, chifukwa, zinthu zomwe dziko limazitcha kupenga, Mulungu amazitcha zodala. Inu muyenera kuti “mutaye malingaliro anu,” kwa dziko ili, chifukwa (chiani?) inu simuli a mdziko lino.

¹⁶² Pamene inu mudutsa mzere wolekanitsa uwo, inu mudzakhala mbadwa limodzi za Ufumu wa Mulungu. O, mai! Ndi zabwino bwanji izo? Bwanji, inu mumakhala cholengedwa chatsopano, (o, mai) osinthidwa kuchokera ku ichi chomwe inu muli tsopano. “Inu muli pano ana aamuna a Mulungu. Tsopano ife tikukhala limodzi mu malo Ammwambamwamba.” Osati, “ife tidzakhala tiri,” mu Zakachikwi. Ife tiri tsopano, pakali pano ife ndife ana a Mulungu. “Pakali pano ife tikukhala limodzi mu malo Ammwambamwamba, mwa Khristu Yesu,” osati mu mpingo mokha, “mwa Khristu Yesu.”

¹⁶³ Ambuye Yesu owukitsidwa ali pano. Iye ali pano mu mphamvu Yake. Iye ali pano mu mphamvu Yake ya chiombolo. Iye ali pano kwa eksodo. Iye ali pano kuti amubweretse membala aliyense wa mpingo mu chiyanjano ndi Iye. Iye ali pano kuti amubweretse wochimwa aliyense, ziribe kanthu kaya ndinu otsika motani, Iye ali pano kuti abweretse mphamvu ya chiukitsiro Chake mu moyo wanu ndi kukupangani inu cholengedwa chatsopano.

¹⁶⁴ Kuno, zaka zingapo zapitazo, zipembedzo zonse za mdziko zinakomana, ine ndikukhulupirira kunali mu London, England, kapena kwinakwake. Ine sindikukumbukira ndendende. Koma, pamene iwo onse anali kuyankhulira mipingo yosiyana, Achimuhamedi, ndi Abuddha, ndi chirichonse. Wamng’ono . . . munthu yemwe ankaimira mpingo wa American Holiness, John Witt, ine ndikukhulupirira, linali dzina lake. Chotero ndiye pamene iye anauka, nthawi yake kuti ayankhule, zipembedzo zonse zoimiridwa mu kusonkhana kwakukulu uku, iye ananena nkhanu ya Dona Maccabee, momwe iye analiri wotsika;

anamangidwa mu Oklahoma, ali ndi ndudu pakamwa pake, akuyendetsa...kapena akuswa lamulo la liwiro, akudutsa mmisewu ndi chikuku. Iye anali atapha kochulukwa kwambiri, ndi moipa kwambiri, ndi mwauve kwambiri, mpaka, pamene iwo anapita kuti akakhuthulire phula ndi nthenga pa iye, iwo sanakhoze ngakhale kuti ayike manja awo pa iye, kuwopa kuti angadetsedwe.

¹⁶⁵ Ndipo pamene iye anatsiriza kunena nkhaniyo mwa sewero chotero, mpaka womvetsera aliyense anali atakhala pamapeto a mpando wawo. Iye anati, “Mabwana, a zipembezoo za mdziko muno, kodi chipembezoo chanu chiri nacho chirichonse chomwe chingayeretse manja a Dona Maccabee?” Palibe yemwe ananena mawu. Iye analumphwa mu malere ndipo anawombetsa zidendene zake limodzi, ndi kuwombetsa manja ake. Iye anati, “Magazi a Yesu Khristu sangayeretse kokha manja ake, koma Iwo angatsuke mtima wake.” Amen. Ndiko kulondola.

¹⁶⁶ Magazi a Yesu Khristu angatenge wachiwerewere wotsikitsitsa mu Louisville, Kentucky, ndi kupanga dona, woyera kuchokera mwa iye. Iwo angamutenge wogulitsa mowa ku malo uko, ndi kupanga njonda kuchokera mwa iye, ndi woyera wa Mulungu.

¹⁶⁷ Abwenzi anga, mbadwa za Ufumu, amuna amzanga amu Kentucky ndi Indiana, ndi kozungulira kuno! Kodi inu simukuganiza, usikuuno, ili pafupi nthawi yoti muwaganizire Ambuye Yesu awa, mwayi wanu wotsiriza usanachotsedwe?

¹⁶⁸ Pamene, inu mukuwuwona Mpingo ukupita mu eksodo yaikulu iyi, kuwona Lawi la Moto likutitsogolera patsogolo pathu; likuima, kumachita zozizwitsa ndi zizindikiro. Iye ali pano, usikuuno, mu mphamvu Yake yonse yowombola. Iye ali pano kuti amupangitse kukhala wamphumphu, wochimwa aliyense, kuti amubwezeretse wobwerera mmbuyo aliyense. Iye ali pano kuti achiritse munthu wodwala aliyense.

¹⁶⁹ Iye ndi Uthenga wathunthu. Ndipo ife timalalikira Uthenga wathunthu; timadya Mwanawankhosa yense. Kumuwotcha Iye ndi Mzimu Woyera, ndi kumadziwa kuti Iye ndi kudya kwabwino, pakuti Mzimu Woyera wapereka kwa ife kuti Iye ndi wabwino kwenikweni. “Talawani ndi kuwona, Ambuye ndi abwino. Iwo amakoma ngati uchi mu thanthwe.”

¹⁷⁰ Ambuye wathu Yesu kuno, mu chikondi Chake ndi mphamvu, mu madalitso Ake aakulu achiombolo! O, momwe Iye akuimira pakati pa mpingo ndi tchimo, usikuuno! Momwe Iye akuimira pakati pa inu ndi chiweruzo; kuukha, kupemphera!

¹⁷¹ Kuno osati kale litali, ine ndinali kuyenda popita mu malo cha kuno mu Ohio, kumene ine ndinali pafupi kuti ndipereke lingaliro langa la chiweruzo. Ine ndinali ndikumakadya kumalo odyera aang’ono a Dunkard. Ife tinali nao msonkhano waukulu. Ine ndimakhala mailosi angapo kunjira mmudzi, ku motelo

yaing'ono. Ine ndinali ndikumakadya ku malo odyera a Dunkard; anthu abwino okondeka, ndipo pa Lamlungu iwo anatseka ndipo anapita ku tchalitchi. Ine ndinachita kupita patsidya ku malo wamba aang'ono, awamba, Achimereka kuti ndikadye chakudya changa chamadzulo.

¹⁷² Pamene ine ndinkayenda polowa pa khomo, mwa kudabwitsidwa kwanga, apo panaima wapolisi waboma ali ndi mkono wake mokumbatira msungwana, akusewera makina opukusa. Tsopano, njuga ndi yosaloledwa mu Ohio, ndipo apo bambo wa lamulo mwiniwake akuswa lamulo. Ndi mwina, bambo wa usinkhu wanga, mwina wokwatira, ali ndi banja kwinakwake; ali ndi mikono yake mozungulira dona wamng'ono wina ataima apo.

¹⁷³ Ine ndinayang'ana mmbuyo modyeramo, anyamata ena atakhala kumbuyo uko, ataledzera, ndi dona wamng'ono asakuchita mwamakhalidwe nkomwe. Ine ndinayang'ana, atakhala pansu, ku mbali ya kumanja kwanga uku, nkanyumba. Komwe, ine ndinali wokonzeka kuti ndikhale pansu.

¹⁷⁴ Apo panali dona wachikulire, winawake wa pafupi usinkhu wa zaka fifite-eyiti, sikisite, wamkulu ngati amayi anga; ali apo, khungu lonse litakwinyika, atavala tizovala tating'ono kwambiri. Ndipo, o, izo zinali moipa. Ndipo zikhadabu zake zakuphazi zitalochedwa papulo, milomo yake italochedwa papulo, mawonekedwe owoneka-mowopsya omwe inu munayamba mwawaona. Tsitsi lake litadulidwa mofupika kwenikweni ndipo liri lokwinyika basi monga *choncho*. Ndipo iye anali akumwa.

¹⁷⁵ Apo panali amuna awiri ali ndi iye, ali apo, owoneka-moipa, ataledzera, ndipo mmodzi wa iwo atagona pa gome. Ndipo pamene iwo anapanga odi, ndi kupita kunja ku chimbuzi. . .

¹⁷⁶ Ine ndinaima apo. Ine ndinaganiza, "O Mulungu, Inu mungakhoze bwanji kupirira nazo izi? Inu mungakhoze bwanji kuyang'ana pa zotero monga izo? Pamene, ngakhale mu mtima mwanga, ndipo ndine woipa monga ndiririmu, komabe, komabe ine ndikudabwa ngati Sarah wanga wamng'ono ndi Rebekah adzayenera kuleredwa mu m'badwo woterowu kuti aziwone izo zikubwerapo. Ambuye, bwanji Inu osangofafaniza izo kuzichotsa pa nkhope ya dziko lapansi?" Ine ndinaganiza, "Inu bwanji osangochita izo, Ambuye?"

¹⁷⁷ Ine ndinakhala pansu apo ndi kungoyamba kumalira. Ine ndinawona masomphenya. Ine ndinawona, monga momwe zinali, dziko likuzungulira mu mlengalenga, ndipo apo panali utawaleza kuzungulira dziko ilo. Ndipo winawake yemwe anali kuyankhula kwa ine, anati, "Awo ndi Magazi a Yesu Khristu, azungulira dziko ili, omwe akumuletsa Iye kuti asaliwononge ilo. Ngati Mulungu angakhoze kuliwona tchimo, 'Tsiku limene inu mudzadya icho, tsiku limenelo inu mudzafa.' Munthu aliyense

ali pansi pa Magazi awo apo, ali . . . ndi ufulu wodzisankhira, kuti utenge kusankha kwako. Koma ngati iwe utafa konse, ndipo solo yako nkukwera kudutsa chifundo cha Magazi awo, iwe waweruzidwa kale iwe usanakafike uko. Palibe kanthu katsalira kwa iwe.”

¹⁷⁸ Ndiye ine ndinadziwona ndekha. Ine ndinawaona Ambuye Yesu anga ataima apo, ali ndi chisoti cha minga pa mutu Wake, ndipo misonzi ikuyenderera pansi, yosakanizikana ndi magari, pamene iwo anali kusambitsa ndevu Zake. Ndipo ine ndinawawona machimo anga akubwera pamaso pa Iye, ndipo nthawi iliyonse iwo amabwera pamaso pa Iye munga choncho, [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]. . . mpaka Iye amakutumula. Minga zimabaya mu zikope Zake, mochuluka. Iye amazandimira mmbuyo. Iye amati, “Atate, mukhululukireni iye, iye sakudziwa zomwe iye akuchita.” Ndipo kachiwiri ine ndimakhoza kuchita chinachake, ndiyeno Magazi Ake amakhala ngati bampala ya galimoto, ikutetezera galimoto, kunditchingira ine ku mkwiyo wa Mulungu, zosandiyenera.

¹⁷⁹ Ndipo ine ndinabwera kwa Iye, mwapang’onopang’ono, ndinagwada pansi kwa Iye. Ine ndinati. . . Ndinayang’ana pansi apo, atagona patsogolo pa ine, ndipo apo panali bukhu lakale la tchimo, ndipo dzina langa litalembedwa pamwamba. Ine ndinati, “Ambuye, kodi Inu mungandikhulukire ine?”

¹⁸⁰ “Ndithudi,” Iye anati, ndi maso achikondi; anafikira ku mbali Yake, anatulutsamo Magazi ena, ndipo analemba pa ilo, “Wakhulukidwa.” Ndipo analiponyera ilo mmbuyo mu Nyanja ya Kwiwala. Iye anati, “Tsopano . . .”

Ine ndinati, “Zikomo Inu, Ambuye.”

¹⁸¹ Iye anati, “Tsopano, ine ndakukhulukira iwe; ndipo iwe ukumuweruza uyo.” O, izo zinasintha chithunzicho, kwa ine.

¹⁸² Ine—ine ndinatuluka umo. Ine ndinayenda kupita uko ndipo ndinakakhala pansi kwa iye, ndipo ndinayamba kuyankhula. Ndipo iye anali ndi moyo wina wovuta mmbuyo mwake. Ine ndinati, “Kodi iwe sunayambe wakhalapo Mkhristu?”

Iye anati, “Ine ndinaleredwa mu banja la Chikhristu.”

Ndipo ine ndinati, “Chinachitika ndi chiani?”

¹⁸³ Iye anandiuza ine za kusiyana ndi mwamuna wake, ndi momwe ana, ndi zina zotero. Ine ndinati, “Konse, mwa zaka zonse izi, iwe sunayambe wakhalapo mwa mtendere chiyambireni pomwe iwe unakomana naye Mulungu?”

Iye anati, “Bwana, izo ndi zoona.”

Ine ndinati, “Kodi inu simumulandira Iye pakali pano.”

Iye anati, “Kodi Iye anganditenge ine?”

Ine ndinati, “Iye akugogoda pa mtima wako pano.”

184 Ndipo kuchokera nkanyumba ako, pansi apo, ndipo anagwada pansi pamaso pa kumvetsera kwa anthu uko; makina opukusawo anaima, kutukwana koipa kunaima, ndi china chirichonse. Ndipo ine ndinakwezera mmwamba manja anga, ndi manja anga. . . ndi manja aang'ono okwinyika awo, ndipo ndinamutsogolera iye kwa Yesu Khristu. Ndiko kulondola. Nzomwe ziri, abwenzi. Musati muziyang'ana. . . Yesu. . .

185 Ine sindikusamala zomwe iwe wachita, momwe machimo ako aliri akuda, momwe moyo wako uliri wamwaye; Mulungu waima, usikuuno, akugogoda pa chitseko cha mtima wako, kuti akukhulukire iwe, ziribe kanthu yemwe iwe uli.

186 Tiyeni tiweramitse mitu yathu miniti. Mlongo, bwerani ku limba apo, mungatero inu?

187 Atate Akumwamba, O, ine ndikupemphera kuti Inu basi tsopano. . . pamene Mzimu Woyera ukuyenda mu nyumba muno. Tiyeni ife tifune poyamba Ufumu, kuti tipeze kukondedwa ndi Iye, ndiye ine ndikukhulupirira Inu muwachiritsa odwala. Koma pakali pano, Atate, pamene ndikumverera kuti pali chidwi chachikulu, chakuya ndi kukhudzidwa, anthu akudziwa kuti Mpingo Wanu uli mu eksodo, ndipo ife tikupita uko ku Chiweruzo. Posadziwa kuti, mmawa, winawake akhoza kudzabwera ku mbali ya kama, ndipo apo titagona, titapita. Nthawi ino, mawa usiku, mwina muli mosungira mitembo kwinakwake, ndipo solo zathu ziri kutsidya mu Muyaya.

188 O Mulungu, ili likhoza kukhala ora lotsiriza! Uwu ukhoza kukhala mwayi wotsiriza umene anthu ati awulandire. Ochuluka, palibe kukaika, ali pano, amuna ndi akazi, omwe akukhumba, omwe akhala moyo wabwino basi wolunga, koma sanabadwe konse kachiwiri, sakudziwa chomwe chimanthauza kukhala wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, moyo wodzipereka kwathunthu; ndi maunyolo onse, manyazi, zitachotsedwa kwa iwo, ndipo Mzimu wa Mulungu utawabatizira iwo mu chifundo Chake.

189 Atate, Wokondedwa, simutero Inu, usikuuno, mu Dzina la Mwana Wanu wokondedwa, Yesu, kusunthira mu mtima uliwonse ndiko kuyankhula pakali pano? Ndipo mulole iwo, mwa kuphweka kwa mtima wawo, akwezere maganizo awo kwa Inu, akweze mtima wawo ndi kuti, "Ine ndiri pano, Yesu. Nditengeni ine tsopano, basi monga ine ndiriri, ndipo ndiumbeni ine ndi kundipanga ine chinachake chosiyana. N dipangeni ine mtundu wa munthu yemwe Inu mukanakhala nane. Monse kupyola mu moyo wanga, Inu mwayankhula kwa ine. Inu mwayankhula kwa ine. Inu mwayesera kuti munditenge ine kuti ndizichita mosiyana. Inu mwayesera kuti mundipange ine kuti ndipange kugonjera uko. Koma tsopano tsiku lapita kwambiri, Ambuye, ndi ine, koma ine ndakonzeka kuti ndibwere pano." Perekani izi, Atate. Pamene chifundo chiri kuitana, Chiweruzo

chisanayambe; eksodo ya Mpingo, kuchoka ku Igupto; mulole iwo abwere, azipita limodzi ndi gulu lalikulu, oitanidwa-atuluke. Ife tikupempha izi mu Dzina Lake.

¹⁹⁰ Ndipo pomwe ife tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa, ndi maso otsekedwa, ndi Akhristu akupemphera. Ine ndikudabwa ngati inu mungakweze mmwamba manja anu, ndi kuti, “M’bale Branham, inu mundikumbukire ine. Ine—ine ndikukhulupirira mawu aliwonse omwe inu mukunena ali Choonadi chokhudza Yesu Khristu. Ndipo ife tonse tikusowa kuti tidzazidwe ndi Mzimu, ndipo, ine sindiri, panobe. Ine ndakhala ndiri membala wa mpingo.” Kapena, mwinamwake inu simukhale muli, nkomwe. Mwina inu mwakhala muli wochimwa, simunamulandire konse Khristu. Kapena, mwakhala muli membala wa mpingo, ndipo simunayambe mwabadwa kachiwiri. Kodi mungakweze dzanja lanu, ndi kuti, “Mundikumbukire ine, M’bale Branham, mu pemphero lanu. Ine ndikufuna ndikhale wolondola.”

¹⁹¹ Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu, ndi inu, ndi inu, inu, inu; ndi inu, m’bale wanga; ndi inu, mlongo; ndi inu, m’bale; inu, inu, inu, m’bale, mlongo. Ine ndikuwona.

¹⁹² O, chakumanzere kwanga, ndi angati mbali ya kuno? Kwezani dzanja lanu, mukuti, “Mundikumbukire ine, M’bale Branham, ine ndikufuna kuti ndibadwe.”

¹⁹³ Tsopano, kumbukirani, Mzimu Woyera ukuyankhula kwa inu. Ngati ine ndiri wantchito wa Mulungu, ine ndikudziwa, motsimikiza monga ine ndaimira pa nsanja ino, kuti Mzimu Woyera ukuyankhula kwa mitima pano. Abwenzi, ine ndikhoza kukhala wodabwitsa kwa inu, koma ine sindine wotentheka. Ine ndikudziwa zomwe ine ndikuzinena; ngati ine nditadziwa lomwe liri vuto lanu kunjira uko, ndi omwe ali matenda anu, ndipo Mulungu akumva pemphero langa kwa inu. Ndipo pomwe pano mu nyumba ino muli anthu omwe achiritsidwa, ndi khansara, ndi akhungu, ndi kugontha, ndi kulumala, ndi china chirichonse. Tayang’anani pa misonkhano kuzungulira mdziko. Nanga bwanji inu tsopano? Nanga bwanji izo tsopano? Ngati Iye akanati amvere pemphero langa kwa izo, kodi Iye samva pemphero langa kwa chikhalidwe cha solo yanu? Ngati Iye akanati aulule kwa ine pamene vuto lanu liri, kodi Iye saulula kwa ine pomwe pali vuto lanu, panonso?

¹⁹⁴ Ndi angati ena omwe muti mukweze dzanja lanu, ndi kuti, “M’bale Branham mundikumbukire ine. Ine ndikufuna, pa nthawi ino, ndimufunse Mulungu kuti akhale wachifundo kwa ine”? Mulungu akudalitseni inu, ndi inu, ndi inu, inu, kachiwiri. O, mai, basi ponse ponse mnyumba, paliponse!

¹⁹⁵ Pamene inu muli ndi mitu yanu yoweramitsidwa. Ine ndikudabwa ngati inu, omwe mwakweza dzanja lanu, mungakhale ndi chisomo china pang’ono pokha, ndi kuti,

“Ambuye, ine ndinali nacho chisomo chokwanira kuti ndikweze dzanja langa, ndipatseni ine chisomo chokwanira kuti ndiime pamene iye akupemphera. Ngati Iye angati andidzere ine, kusanati kuche, Ambuye, ichi ndi chisonyezo changa kwa Inu, kuti ine ndikufuna kukhala wolondola. Ine ndikufuna kuti ndidzakomane ndi Inu tsiku lina. Chifuwa ichi chifika mmwamba mwa mikono yanga ndipo ine ndidzatsamira mtsamiro woferapo. Adotolo adzachoka pa mbali ya kama yanga; palibe choti chingachitidwe. Ndiye, Mulungu, chitirani chifundo solo yanga. Pomwe chifunga chozizira cha imfa chikuyandama mu chipinda, mulole chombo chakale chaku Zioni chidzabwe, chidzandinyamule ine ndipite. Ine ndidzaima, Ambuye. Izo zikutengera chisomo chochuluka, koma Chinachake chikundisuntha ine. Ine ndikuima.” Mulungu akudalitseni inu, m’bale.

¹⁹⁶ Winawake aime, ndi kuti, “Ine ndikuima, Ambuye.” Mulungu akudalitseni inu, m’bale. Mulungu akudalitseni inu, m’bale, mlongo. Ingokhalani chiimire. Aliyense yemwe akufuna kuti akumbukiridwe mu pemphero ili, kwa chipulumutso cha solo yanu, kodi inu mungaime. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu, bambo wamng’ono. Mulungu akudalitseni inu, bwana. Mulungu akudalitseni inu, m’bale. Mulungu akudalitseni inu, mlongo wanga. Mulungu akudalitseni inu, mlongo; inu, m’bale.

¹⁹⁷ Winawakenso akuima tsopano ndi kuti, “Ndi ine pano. M’bale Branham, ine sindikuimirira pamaso pa inu. Ine ndikuimirira pamaso pa Mulungu. Chinachake chandiuza ine kuti ndiime, ndipo ine ndikuima.” Kodi inu mungachite izo? Mungoima pa mapazi anu. Mungomutenga Mulungu mochuluka choncho. Mulungu akulitseni inu, dona.

¹⁹⁸ Alipo enanso. Mulungu akudalitseni inu, dona. Ndiko kulondola. Mayi osauka amugwira mwana wawo wamng’ono, akuyesa kuti adzuke, misozi mmaso mwawo. Kodi inu simubwera? Imirirani kachiwiri. Mulungu akudalitseni inu, dona, dona wachikulire anaimirira apo, ndi wachikulire kwenikweni, podziwa kuti iye ayenera kudzaonana ndi Mulungu, limodzi la masiku awa. Mulungu akudalitseni inu. Ndani ati aimirire motsatira tsopano, akuti, “Ine ndiimirira?”

Ingotsalani chiimire kwa pemphero.

¹⁹⁹ Winawakenso? Ine ndikungomverera ngati pali winawake yemwe akufuna kuti aime. Mwina inu mukungofuna kuti muyandikire pang’ono. Musati muchiike kumbali ichi kenanso. Ingoimirirani. Mungatero inu? Inu omwe mukufuna kuti muyandikire kwa Mulungu. Mulungu akudalitseni inu. Ndiko kulondola. Wina angati... Mulungu akudalitseni inu, dona. Inde, bwana.

²⁰⁰ Alipo pafupi anthu ena atatu, ine ndikuwayang'ana molunjika ndithu, akuyenera kuti aimirire, chifukwa apo paima Mngelo wa Mulungu. Mulungu akudalitseni inu, dona. Ndiko kulondola. Tsopano, chabwino, m'bale, nanga bwanji izo? Chabwino. Ndipo, Mngelo wa Ambuye waimirira, ine ndikudziwa. Ine ndikuziwona Izo, ndipo ine ndikudziwa kuti winawake akuyenera kuti aimirire pakali pano. Ine ndidikirira utali wa miniti yokha. Mulole Mulungu. . . Inu mukudziwa Iye akufinya pa mtima wanu. Iye waima pamenepo, bwenzi wanga. Ndi Iyeyo yemwe akukuuzani inu kuti muimirire. Kodi inu simuchita izo? Ingoimirani ndi kumulandira Iye, pakali pano. Chabwino.

²⁰¹ Kodi inu mukutsimikiza tsopano? Ngati Mulungu angakuitaneni inu usikuuno, mu msonkhano uno; ulaliki uwu, kuitana uku, kudzakumana nanu uko pamene inu mudzafa. Kodi inu mwachita nazo chiani izo? Ngati inu simuli otsimikiza, zedi, imirirani tsopano, kotero kuti Iye akuoneni inu mukufuna kumulandira, kuti muziyenda mu Kuwala.

²⁰² Tsopano, Atate athu Akumwamba achifundo, ana Anu okonedwa awa, mitima yofewetsedwa, Mawu agwera mu mtima mwawo usikuuno. "Chikhulupiriro chimadza pa kumva, ndipo kumva kwa Mawu." Ndipo iwo akhoza kumva. Ndipo Inu mwafewetsa mitima yawo, ambiri aimirira, amuna ndi akazi, anyamata ndi asungwana, akuvomerezani Inu ngati Mpulumutsi wawo wawo ndi Mtsogoleri.

²⁰³ Ndipo mulole Mngelo wa Mulungu, Yemwe ali pano usikuuno, Iye atawatsogolera iwo kupyola mu moyo. Mulole iwo atsogoleredwe waku Kalvare pakali pano, mu mitima yawo, ndipo amulandire Yesu ngati Mpulumutsi wawo. Ndipo mulole Mzimu Woyera, kupyolera mu Magazi a Khristu, ubwere pa miyoyo yawo, ndi kudzachotsa kusiyana kwawo konse, ndi kuwadzazitsa iwo ndi ubatizo wa Mzimu Woyera. Mulole uno ukhale usiku waukulu wa moyo wawo. Iye tikudziwa iwo uli, pakuti usiku uno iwo akukulandirani Inu. Perekani izi, Ambuye, pakali pano. Ndipo mulole iwo azipita kwawo kuchokera kuno, usikuuno, okondwa ndi osangalala, akutamanda Mulungu, ndi mtima wawo wonse. Ine ndikupempha dalitso ili kupyolera mu Dzina la Yesu Khristu.

Tsopano Ambuye atakudalitsani inu pamene muli kukhala.

²⁰⁴ Ndiroleni ine ndikufunseni inu tsopano. Mmodzi aliyense wa inu yemwe anaima, ndipo inu mukudziwa kuti chinachake chachitika kwa inu pamene inu munali mutaima, kwezani dzanja lanu. Mungokweza dzanja lanu, amene mukudziwa chinachake chachitika. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Ndiko kulondola. Izo ziyenera kutero, abwenzi. Izo ziyenera kutero. Ine ndinaima, ndinawona pano posachedwapa, Mngelo yemwe uja yemwe ine ndimamukamba,

akupita kudutsa mnyumba muno kuno; Mngelo yemwe uja wa Ambuye, Lawi la Moto. Ine ndakhala ndikulalikira maminiti asanu otsiriza kapena khumi, pansu pa kudzoza uko. Ine ndikumumverera Iye, kungomuwona Iye akuyenda kupyola mu chipinda chino. Tsopano, inu mukhoza kuganiza kuti ine ndikunena nthano kwa inu, koma ndi Zoonadi.

²⁰⁵ Tsopano, ine sindikuganiza ine ndiitanitsa nkomwe mzere wa pemphero. Ine ndikuganiza ine ndingoima pomwe pano ndi kungomufunsa Mulungu kuti atsimikizire kuti zomwe ine ndimakuzani inu ndi Zoonadi, ndiko kulondola, ndi zizindikiro, zodabwitsa.

²⁰⁶ Ndi angati muno akufuna kuti achiritsidwe, anthu odwala? Kwezani manja anu, paliponse pomwe inu muli. Mungokweza dzanja lanu, ndi kuti, “Ine ndikuwalandira iwo.” Chabwino.

²⁰⁷ Ine ndikufuna kuti inu muyang’ane, mukhale moyo, ndi kukhulupirira. Winawake mwa omvetsera awa, kudutsa *apa*, winawake kupyolera *apa*, angoyang’ana, ndi kuti, “Ambuye Yesu. . .”

²⁰⁸ Monga chonchi. Ine ndikukhulupirira, chifukwa chomwe ine ndinaitanira ku guwa kuja poyamba, ife tikuyenera kuti tipeze chisomo ndi Iye. Ichi ndi chinachake chatsopano kwa ine. Ine ndiyenera kuti ndipeze chifundo ndi Iye, poyamba. Ndiye ngati ine ndapeza chifundo, ndi kuchita mwachifundo. . . Ndipo inu, dazeni, kapena iwiri, miyoyo nkubwera kwa Iye apo pomwe. Ndithudi, ndithudi. . .

²⁰⁹ Tsopano, wina aliyense wa inu anthu omwe mwabwera kwa Khristu, ndiye, mukapeze mpingo wabwino wodzazidwa ndi Mzimu Woyera ndipo muzikapita kwa iwo. Ndipo uko mukafunefune ubatizo Wake mpaka inu mutaupeza Iwo; muzikangopita, basi usiku uliwonse, tsiku lililonse, muzikangomapemphera. Ndipo pomwe inu mukuyang’ana. . .

²¹⁰ Tsopano, inu anthu omwe mukudwala. Ngati ine ndakuuzani inu Choonadi, Mulungu achitira umboni kuti izo ndi Zoonadi. Ndiko kulondola. Angochita kokha izo. Ndipo Mulungu azipanga izo kudziwika, ngati inu muti mungopemphera ndi kukhulupirira ndi mtima wanu wonse. Mungoyang’ana, ndi kunena izi. . .

²¹¹ Pamene Mngelo wa Ambuye anakomana ndi ine kunjja uko ku Chigayo cha a Green, Indiana, zaka eyiti zapitazo; kuchokera pamene ndinali mwana, wanditsatira ine, wandisonyeza masomphenya. Pamene ine ndinapita kwa Iye. Iye anati, “Ngati iwe uti ukhale woonamtima, nkuwatengera anthu pokukhulupirira iwe, palibe kanthu kati kadzaima patsogolo pa pemphero lako.”

²¹² Tsopano, Iye akhoza kuchita zomwezo kwa inu tsopano zomwe Iye anakhoza kuzichita uko. Iye wawuka kwa akufa. Ndipo Iye. . . uko omvetsera kunjja uko pamaso pa Iye. Iye

akudziwa zomwe ziri pa wina aliyense wa inu, zomwe inu mwachita, lomwe liri vuto lanu, chirichonse cha izo. Kodi inu mukukhulupirira izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndiye mukhulupirire izo ndi mtima wanu wonse.

²¹³ Ine ndikuzindikira bambo wamng’ono wakhala apa, akukhulupirira, akuyesera kutero, kukhala ndi chikhulupiriro. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu andilola ine kuti ndidziwe chomwe chiri chovuta ndi inu? Inu mutero? Ngati Iye ati atero, kodi inu mulandira machiritso anu? Inu muli ndi vuto la mtima. Sikulondola uko? Bwanji ngati ine ndikanakuuzani inu tsopano kuti muli abwino kwa izo zonse? Kodi inu mungakhulupirire izo? Imirirani miniti yokha. Inu muli ndi mtima wamanjenje, ndi mtima wong’ung’uza. Izo zakusautsani inu kwa nthawi zina. Nthawi yokha, pamene inu mugona pansi, aponso, izo zimakubanikitsani inu, ndipo inu mumakhala ndi kugunda kochuluka mmbuyo ndi mtsogolo, kuthamanga. Ndi kulondola uko? Chifukwa, izo zimayambitsa kusagaya mmimba mwanu, kumabwera kupyolera mu msempha uwo. Si kulondola uko? Inu simusautsidwanso ndi izo kenanso. Ingsungani chomwe inu muli nacho pakali pano; inu mukhoza kupita kwanu ndi kukakhala bwino.

²¹⁴ Ine sindiri kuwerenga maganizo anu. Ndine mlendo mwangwiro kwa inu. Inu mwangokhala bambo muli apo. Ndi kulondola uko? Sindinayambe ndakuonani inu mu moyo wanga, ndipo sindinadziwepo konse kanthu ka inu. Ndi zoono izo? Khulupirirani kuti Ambuye ali pano!

²¹⁵ Moona, mnyamata, ine ndikufuna ndikufunse iwe chinachake, ndipo iwe uwone ngati ichi chiri choonadi kapena ayi. Pafupi mphindi pang’ono zokha zapitazo, zonse mwadzidzidzi, chinachake chachirendo chinabwera pa iwe pamene ine ndinayamba kuyankhula za “cholumira kuchoka mu mbola.” Kodi si kulondola uko? Kodi iko sikunali kumverera kwachirendo komwe iwe unali nako, utakhala apo? Sikulondola uko? Ndipo kodi iwe siunayang’ane kwa ine pa nthawi yomweyo iyo, ndipo maso anga anakugwira iwe pa nthawi yomweyo? Ndi pamene iwe unachiritsidwa, ndi vuto lako la mtima, apo pomwe. Amen. Ndizo ndendende. Iye ali pano.

²¹⁶ Ine sindiri kuwerenga maganizo anu, abwenz. Ine ndikuyankhula kokha Choonadi, ndipo Mulungu akuzitsimikizira izo kukhala Zoonadi.

²¹⁷ Kodi inu mukuganiza chiani za izo, mwakhala apo pafupi ndi iye? Kodi inu mukukhulupirira? Kodi inu mukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri wa Mulungu? Kodi inu mukukhulupirira ngati Mulungu... Inu mwakhala patsogolo, kuno pa mpando wapatsogolo, ndi chifukwa chake ine ndikuyankhula kwa inu mochuluka kwambiri, poziwona Izo mmbuyo kuseri uko ndi pondizungulira ine. Koma kodi inu

mukukhulupirira, ngati ine ndingakhoze kuwugwira mzimu wanu, Mulungu awulula chomwe chiri chovuta? Kodi inu muwalandira machiritso anu? Ndinu wa matenda a shuga. Ndi kulondola uko? Kwezani mmwamba dzanja lanu ngati izo ziri. Imirirani pa mapazi anu. Kodi inu mukuwalandira machiritso tsopano? Mulole Ambuye Yesu Khristu akupangeni inu gawo lililonse wamphumphu. Mulungu akudalitseni inu.

²¹⁸ Mukhale ndi chikhulupiriro. Winawake *muno* akukhulupirira. Mukhale nacho chikhulupiriro, ndi mtima wanu wonse.

²¹⁹ Ine ndikuwona bambo wamng'ono wakhala uko atavala suti ya buluu. Apo Iye waima pamwamba pomwe pa iye. Inu muli ndi matenda a pakhungu, sichoncho inu, bambo wamng'ono? Si kulondola uko? Imirirani pa mapazi anu. O, ine ndikuwona, inu ndinu a nthumwi izi. Ndi kulondola uko? Chabwino, kodi inu mukufuna mupite kwanu muli bwino? Kwezani mmwamba dzanja lanu ndi kuti, "Ambuye Yesu, ine tsopano ndikukhulupirira Mngelo wa Ambuye akutsogolera mopitirira. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti ine ndachiritsidwa."

²²⁰ Kodi inu mukuganiza chiani pa izo, bambo wotsatira kwa iye apo, kodi inu mukukhulupirira, nanunso? Imirirani pa mapazi anu miniti, chotero ine ndikhoze kumayang'ana pa inu. Inu mukundikhulupirira ine kuti ndine wantchito wa Mulungu; ndi mtima wanu wonse? Inu mukufuna kuti muthane nalo vuto lanu la mtima ilo? Ndicho chomwe inu munali nacho, si choncho? Ndi chomwe inu "*munali nacho*," ine ndinatero. Inu mulibe icho tsopano. Inu mukhoza kupita kwanu, nanunso.


²²¹ Bambo wotsatira kwa iye, kodi inu mukuganiza chiani za izo, bwana? Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Kodi inu mukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri wa Mulungu? Imirirani pa mapazi anu. Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse tsopano? Inu munali ndi manjenje. Si kulondola uko? Mwaona? Ndi kulondola uko? Kwezani mmwamba dzanja lanu. Inu mukhoza kupita kwanu muli bwino tsopano. Yesu Khristu wakupangani inu kukhala bwino.

²²² Nanga bwanji bambo wotsatira, mwaima, mopitirira ndi mzere, kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Imirirani pa mapazi anu. Kodi inu mukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri wa Mulungu, kuti ine ndi wantchito Wake? Kodi inu mukukhulupirira Iye angandiuze ine chomwe chiri chovuta ndi inu, kuti inu mungalandire machiritso anu? Ilo liri pa mmero wanu. Ndi kulondola uko? Pitani kwanu ndi kukhala bwino, mu Dzina la Yesu Khristu.

²²³ Wina aliyense mu nyumba muno, yemwe akufuna kuti akhale bwino, akhoza kuuka ndi kuchiritsidwa. Ngati inu mukundikhulupirira ine, ngati wantchito wa Mulungu, imirirani pa mapazi anu. Mulungu akudalitseni inu. Vuto lachikazi,

khansara, apo iyo ikupita. Mulungu adalitsidwe! Wina aliyense wa inu, kwezerani manja anu kwa Mulungu.

²²⁴ Atate athu Akumwamba, ine tsopano ndikutsutsa nthenda iliyonse ili mnyumba muno, kutulutsa mzimu woipa uliwonse, ndipo mulole Mzimu Woyera utenge ulamuliro tsopano ndi kumupanga munthu aliyense kukhala bwino.

²²⁵ Ikani manja anu pa wina ndi mzake, ndi kumati, “Ambuye alemekezeke,” paliponse. Ndipo muzisangalala ndi kukondwa, pakuti Yesu Khristu ali pano, Mwanawankhosa wa Mulungu, kuti akupangeni inu kukhala bwino, wina aliyense. 

CHIOMBOLO MWA MAGAZI CHA54-0329
(Redemption By Power)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham wolalikidwa mu Chingelezi pa Lamlungu usiku, Marichi 29, 1954, ku Male High School mu Louisville, Kentucky, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa mchaka cha 2006 ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©2006 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org